


# CHIFUKWA CHIYANI

## BETELEHEMU WAMNG'ONO?

 Zikhoza kuwoneka zokhala ngati zoseketsa, mmawa uno, kuvala chikhoto changa pa nsanja, koma ine ndinali wokondwa kwambiri ku—kuwonetsera chikhoto chokongola icho chimene mpingo wandipatsa ine. Ine ndinamuwona M'bale Neville kuno tsiku lina, atavala suti yabwino iyi, momwe iyo inamukwanira iye mwabwino kwambiri, ndipo ine ndinaganiza, chabwino, ine . . . Iyo imawoneka bwino kwambiri, ndipo osonkhana akulankhula za iyo, ine ndinaganiza, “Ine ndidzangovala chikhoto changa pa nsanja.”

<sup>2</sup> Inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira kuti ife sitimakula. Ife nthawizonse . . . Ndipo ine sindikufuna kukula. Bwanji za izo, M'bale Luther? Ayi, sindikufuna kukula, ife tikungofuna nthawizonse kukhalabe ana.

<sup>3</sup> [M'bale Neville anena, “M'bale Branham, ine ndimaganiza kuti inu munavala zina za zovala zija monga atumiki a kalasi-yapamwamba awa. Ine ndinangopenya ngodya ya diso langa, ndipo ine ndinaganiza mwina inu mwavala mkanjo.” M'bale Branham ndi osonkhana aseka—Mkonzi.] Kuyamikira ku chikhoto chabwino icho.

<sup>4</sup> Chabwino, ine ndidzanena kuti ndiyo—ndiyo . . . Ine ndinali kufuna imodzi moyipa kwambiri, ndipo ndiyo yabwino yomwe ine ndinakhalapo nayo. Ndipo ine ndithudi ndikuyamikira izo. Ndipo M'bale Roy Roberson, ine sindikudziwa ngati iye ali pano mmawa uno kapena ayi, iye anali nacho chinachake chochita ndi kusankha kwa izo. Ndipo iko kwenikweni kunali kusankha kwabwino, ndipo ife tiri—ife tiri kwambiri—kwambiri okondweretsedwa kukhala nazo izo.

<sup>5</sup> Ndipo kotero ife tiri okondweretsedwa kwambiri kubwerera mu nyumba ya Mulungu wamoyo, mmawa uno, ndi kusangalala nazo nthawi zodabwitsa izi za—za chiyanjano pozungulira Mawu Ake ofunika.

<sup>6</sup> Ndipo ndi posachedwa tsopano, ngati Ambuye alola, ine ndiyenera kupita kutsidya kwa nyanja. Ndipo ine ndikuganiza kuti inu munaziwona izo mu *liwu* la Anthu Amalonda, kuti ine ndipita kutsidya kwa nyanja mwezi wamawa uwu. Ndipo ife tidzakhala tikupempha mapemphero onse a anthu, kuti iwo adzatipempherere ife pamene ife tiri kutali. Ndi zowoneka kuti kutsidya kwa nyanja misonkhano yanga imawoneka kuti ndi yabwinoko, chifukwa iyo imatengedwa bwino kumeneko. Mu America . . .

<sup>7</sup> Ine ndinali kumuuuza M'bale Mercier kuti ine ndinamvetsera kwa...Iye anandipatsa ine rekodi puleya, poyamba, ndipo iyo inali nawo marekodi pa iyo, ya ena a maualiki anga. Ine ndinadziwa ndiye, ngati aliyense anamverapo kwa ine, chikanayenera kukhala chisomo cha Mulungu kwa iwo, chifukwa ine ndimaganiza kuti ine ndikhoza kukhala wabwinoko pang'ono.

<sup>8</sup> Iye akujambula izo, apanso. Pa—pang'ono, inu mukhoza kudula gawo ilo, onani. Kapena, iye wakanikizira chala chake chachikulu panso, ine ndikuganiza ndiko kudula izo.

<sup>9</sup> Koma ine—ine ndikukuuzani inu, ine ndinali wodabwitsidwa kwambiri. Ine...Kulalikira kosakhala bwino kumene ine ndinayamba ndakumvapo mmoyo wanga, kunali kwanga komwe, ndiko kulondola, pa—pa—pa rekodi. Ine...Izo zinandipangitsa ine manjenje zedi, ine sindinakhoze ngakhale kudya chakudya changa chamadzulo. Ine ndinadwala kwambiri, ndinachoka pa thebulo, sindinakhoze kugona usiku umenewo.

<sup>10</sup> Ndipo ndinapita mu Kentucky, ndi M'bale Wood dzulo. Tikubwerera, ine ndinati, "M'bale Wood, ine sindikuwona momwe ine ndimapezera anthu kuti abwere ndi kudzandimva ine ndikulankhula. Ndizo kwambiri—kwambiri zosakhala bwino, kudzi bwereza ndekha chotero, ndipo, o, galamala kusowa, ndi, zopumira, palibe—palibe chirichonse." Ine basi... Ine sindikudziwa. Ine ndinati, "Izo zinandilimbikitsa ine mu njira yina, kudziwa kuti ayenera kukhala Mulungu, kapena aliyense sakanamabwera konse." Ndiko kulondola.

<sup>11</sup> Kotero ine ndinali kulankhula kwa M'bale Collins. Ine ndikuganiza kuti iye ali mnyumba muno. Ndipo kotero ine ndinanena kwa iye...Iye anabwera uko, ndipo ndinali kumuuza iye za izo. Ine ndinati, "M'bale Collins, ine moona mtima..." Ine ndinati, "Ine ndiri pafupi kwenikweni zaka makumi atatu zakubadwa, ngati mlaliki, ndipo ine ndithudi ndiyenera kudziwa chimene ulaliki uli." Ine ndinati, "Ndiwo wosakhala bwino umene ine ndinawumvapo."

<sup>12</sup> Ndipo iye—iye ndi mtumiki wa Methodisti, ndipo m'bale wake ndi munthu ndithu mu chipembedzo cha Methodisti. Ndipo iye anati, "Chabwino," iye anati, "Ine ndikuuuzani inu, M'bale Branham," anati, "zopumira ndi—ndi ziganizo zanu zikhoza kusatha bwino, ndi zinthu monga choncho, koma," anati, "kodi inu munayamba mwaganizapo za mnyamata uja amene analalikira pa Tsiku la Pentekoste, amene sankakhoza ngakhale kulemba dzina lake lomwe—dzina, dzina lake linali Petro?" Anati, "ine ndikuganiza kuti iwo sunayikidwe zopumira molondola kumene."

<sup>13</sup> Koma, inu mukuona, chimene chimampangitsa munthu kuyika maso ake pa izo, inu mumamvera kwa zolengeza za pa wailesi izi, ndi izo zonse zimene zalembedwa, inu mukuona.

Ndipo iwo—iwo akhoza kulemba izo ndi kuyika zopumira izo, ndi zinthu, chifukwa iwo akuwerenga izo.

<sup>14</sup> Ine ndinayima ndi Charles Fuller, akulalikira kuseri kwa bwato monga *choncho*, ngati nsanja yake. Ndipo chirichonse chimene iye ananena, iye ankawerenga izo mpaka pansu, nambala wani, nambala thuwu, nambala firii, nambala folo, monga *choncho*, mpaka iye anatsiriza zonse bwino, nazikonza mwanthawi izo. Ndipo izo zinali zonse zofufuzidwa, kufufuzidwa pa wailesi, ndi chirichonse.

<sup>15</sup> Chifukwa, ndi Billy Graham, ine ndinawona wake, ndi zina zotero, pamene iwo amangoyima pamenepo nalankhula izo, kungowerenga izo chabe mwaliwiro monga iwo angakhozere kuwerenga izo, ndipo izo zonse nzokonzeka, kotero ine ndikuganiza inu mukhoza kukhala nazo zopumira.

<sup>16</sup> Koma vuto la ine, ine sindingakhoze ngakhale kuziwerenga izo. Kotero, ndipo ngati ine ndikanalemba izo, ine ndikutsimikiza ine sindikanakhoza kuziwerenga izo. Kotero ndicho chisomo chodabwitsa, sichoncho, kuwona chimene Iye akhoza kutichitira ife. Koma ine ndiri woyamikira kuyambira mkati tsopano, kuthera kwa chaka chakale ichi, kuti tiyambe chaka chatsopano.

<sup>17</sup> Ine ndinamvera kwa mzera wa pemphero, ndipo ine ndithudi sindinali wokhutitsidwa ndi mzera wa pemphero, ngakhalenso, kumvetsera kwa izo. Ndiyo nthawi yoyamba imene ine ndinadzimvapo ndekha monga *choncho*, kwa—kwa uthenga, ndipo ine ndithudi ndinali wodabwitsidwa, mizera ya pemphero siyikuyenda molondola. Ayi, ine ndikuganiza izo zidzachitika kuti, patapita kanthawi, izo zidzakhala chomwecho kuti aliyense adzayenera kudziwa chirichonse za izo iwo asanakhulupirire. Ndipo kuyambira koyamba kwa chaka, ine ndikufuna kusintha izo, ndipo kungoyamba mzera wa pemphero paliponse pamene Mulungu alankhula kwa ine, “munthu *uyu* wachoka pa mzere,” kapena chinachake cholakwika, ine ndidzayima naye iye. Kulola ena onsewo kupita mopyola, chifukwa iwe sumatenga okwanira kuti adutse chotero, onani. Anthu amadziwa pamene iwo ali, ndi omwe iwo ali, ndi chimene iwo achita. Koma iwo amapeza chinachake chimene sichinafole molondola chabe ndi Mulungu, ndiyo nthawi yoyima pa chimodzi icho, nkunena, “*ichi* ndi chimenecho,” onani. Kotero ine ndikuganiza mwina pakhala kusintha kwina kumene kuti kuchitike, M'bale Leo, pakuti ine ndinawamva iwo, ndipo ine ndikudalira kuti Mulungu adzatithandiza ife mu chaka chikubwerachi.

<sup>18</sup> Tsopano, ine ndikukhulupirira kuti usiku uno iwo ali nayo misonkhano kuno ku Kachisi. Ndipo ine ndiri woti ndidzakhale kuno pa 62, ndi M'bale Ruddell, usiku uno. Ine ndikumva kuti iwo akhala nawo utumiki wa ulonda pano. Ndipo M'bale

Ruddell anandifunsa ine za utumiki wa ulonda uwo, koma ndikuganiza mwina ine ndidzabwerera ku Kachisi chifukwa cha usiku umenewo, chifukwa ine nthawizonse ndayesera kukhala pa Kachisi pa—pa kulowa kwa chaka chatsopano, ndipo ine ndimafuna kubwereranso kuno ndi abale apa. Kotero ine ndinakhala ngati ndanyengerera pang’ono, ndipo ine ndidzakhala naye M’bale Ruddell usiku uno, kuja pa 62, ku Kalabu yakale ya 62 imene yatembenezidwa kukhala—mpingo. Ndiyeno Lachitatu usiku tidzabwerera pano pa utumiki wa ulonda. Ndiyeno Lachinai ife tidzanyamuka waku Chicago, ndiyeno mpaka, ndipo mpaka ku Philadelphia, ndipo kenako kutsidya kwa nyanja.

<sup>19</sup> Ndipo mmawa uno, ife sitikufuna kukusungani inu motalika kwambiri, chifukwa ndiwo . . . ife tiri nazo zokambirana, ndipo misonkhano ikupitirira.

<sup>20</sup> Ndipo, nmena, chichitikireni msonkhano wotsiriza wa pemphero pano, o, ine ndiri woyamikira chifukwa cha zotsatira zimene zinabwera kuchokera ku msonkhano wotsiriza wa pemphero. Icho chinali ndithudi chinthu chodabwitsa chimene Ambuye wathu angakhoze kuchita pamene anthu Ake asonkhana pamodzi. “Iwo amene ali . . . adzayitana pa Dzina la Ambuye, kudzisonkhanitsa okha palimodzi,” ine ndikukhulupirira ili njira yomwe izo ziliri, “ndipo—ndi kupemphera, ndiye Mulungu adzamva kuchokera Kumwamba.”

<sup>21</sup> Kotero tiyeni ife tiweramitse mitu yathu, mphindi chabe tsopano, pamene ife tikuyang’ana kwa Iye kuti atipatse ife kudzoza kumene kukusoweka kwa Uthenga uwu.

<sup>22</sup> Ambuye, Inu mwakhala pothawirapo pathu ndi mphamvu mu mibadwo yonse. Makolo athu, ife tisanakhale, anadalira mwa Inu, ndipo iwo sanadabwitsidwe. Iwo ankakhulupirira mu Dzina Lanu Loyera, ndipo iwo anabweretsedwa ngati nyali zowala; ndipo ife tikuyang’ana pa iwo, monga ndakatulo yanena, “Mapazi pa mchenga wa nthawi; kusiyana kwathu kumasiya mmbuyo mwathu, mapazi pa mchenga wa nthawi.” Ndiye ife tikuwona kuti iwo amene anadalira mwa Inu, nthawizonse, popanda nthawi imodzi kulephera, anatuluka bwino. Ngakhale iwo anapyola mu madzi ambiri akuya ndi—ndi mayesero aakulu ndi mazunzo, komabe, pa mathero, Inu nthawizonse mumawatulutsamo iwo “oposa agonjetsi,” chifukwa iwo ali Mawu Anu olonjezedwa kuti Inu mukachita izi.

<sup>23</sup> Ndipo ife tipemphera, lero, kuti Inu mudalitse mpingo wawung’ono uwu. Mdalitseni m’busa wake, m’bale wathu wabwino, M’bale Neville, ndi banja lake. Ife tikupempha kuti Inu mudzangokhala naye iye mu chaka chikudza ichi, ndipo mudzamudzoza iye kwakukulu ndi—ndi kumudalitsa iye mu njira iliyonse. Limbikitsani thanzi la banja lake, aang’ono amene akukula. Msungeni M’bale Neville wamphamvu ndi wathanzi.

<sup>24</sup> Ndipo dalitsani mpingo uwu ndi membala aliyense amene ali mmenemo. Gulu la matrastii, momwe ife timawakondera iwo monga amuna olimba kwenikweni a Mulungu; ndi gulu la madikoni, iwo ali nawonso atumiki Anu amphamvu. Ndi anthu onse amene amabwera kuno, ife tiri oyamikira chifukwa cha iwo, Ambuye. Zimangochitira ubwino mtima wanga kudziwa kuti dziwe laling'ono lakale ili ndi chidutswa cha msipu chitayima pa ngodya, zaka zambiri zapitazo, chapangidwa nyumba ya kuwunikira ku Ufumu wa Mulungu. Ndipo ine ndikupemphera, Mulungu, kuti iyo idzayime mpaka Yesu atadza. Ndipo mulole miyoyo yambiri yayikulu imene yakhala muno, Ambuye, idzatulukire pa Tsiku limenelo, yotsukidwa mu Magazi a Mwanawankhosa. Perekani izi.

<sup>25</sup> Ndipo pamene ife tikutsegula Mawu odalitsidwa Anu awa, mmawa uno, Ambuye, pakutembenezira kumbuyo masamba kuti tiwerenge kuchokera kwa Ilo phunziro, ndipo ife tikudziwa kuti Inu nokha mukhoza kutipatsa nkhani yake. Ndipo ife tikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudzadzoze Mawu Anu, mulole kuti Iwo apite molunjika ku mitima ya anthu amene adzawachitire iwo zabwino. Mupange okhulupirira kuchokera mwa osakhulupirira; ndipo limbikitsani Akhristu; ndipo chiritsani odwala; ndipo perekani kulimbika kwa okhumudwa; ndipo mutengere ulemerero kwa Inueni. Kutu tichite izi, Ambuye, dulani milomo imene iti ilankhule ndi makutu amene ati amve. Pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

<sup>26</sup> Kulengeza nkhani yaying'ono imene ine...inagwera pa mtima wanga kuyambira Lamlungu lapita. Ndipo ine ndinali kulankhula za amuna anzeru kubwera ku—kudzamuwona Yesu, Nyenyezi yomwe iwo anayitsata kuchokera Kummawa mpaka Kumadzulo; ndikuwerenga izo, ine ndinagunda Lemba, ndiyeno ndinapezeka kuti sindinali pano pa kulowa kwa Khirisimasi chifukwa cha utumiki wina wa kundende, ndi zinazotero, ine ndimayenera kukhalako. Ine ndinaganiza kuti ndidzalankhule lero pa phunziro la: *Chifukwa Chiyani Betelehemu Wamng'ono?*

<sup>27</sup> Ndipo ine ndikufuna kuwerenga kuchokera m'Bukhu la Mika, mneneri, mmodzi wa aneneri aang'ono, mutu wa 5 ndipo ndime ya 2. Iwo umawerengeka monga chonchi.

*Koma iwe, Betelehemu Efrata, ngakhale ndiwe wamng'ono pakati pa zikwi za Yuda, koma kuchokera...komabe kuchokera mwa iwe adza... bwera kwa ine wina iye wakuweruza... wakudzakhala woweruza mu Israeli; amene maturukiro ake akhala kuchokera...kale, kuchokera ku nthawi zosatha.*

<sup>28</sup> Ine ndinali nawo malo pa Lemba pamenepo, ndicho chifukwa ine sindikanakhoza kudziwa chimene mawu anali, pa nthawi.

<sup>29</sup> Mwa malo onse amene ali mu Palestina! Ndipo mmenemo muli mizinda yayikulu yochuluka kwambiri, ndi malo ake, mizinda imene ili mwakuwoneka yodziwika mochuluka koposa mwa kuphunzira kwa mbiriyakale, ndi yotetezedwa bwino mizinda yaikulu. Ndipo chifukwa chiyani kuti Mulungu asankhe Betelehemu wamng'ono kuti akhale malo obadwirako Mwana Wake? Ilipo yambiri yomwe ili yayikulupo. Ndipo mwa chitsanzo, kuphunzira kwa mbiriyakale kwa Yerusalemu, Yerusalemu wosangalatsa, likulu la iyo yonse, ndipo ndiwo umodzi wa mizinda yayikulu kwambiri ya Palestina. Ndiyeno ife tikudabwa chifukwa chiyani Mulungu angatenge tawoni yaying'ono kwambiri iyo ya Betelehemu, kuti akhale malo obadwira Mwana Wake.

<sup>30</sup> Koma monga Malemba anena, “Chimene Mulungu alinga kuchichita, icho chidzachitidwa.” Ndipo alipo Mulungu, anazikonzeratu izo kuti zidzakhale mwa njira iyo kapena izo sizidzakhala konse mwa njira iyo. Ndipo apo Lemba likunena, mu mutu wa 15 wa Machitidwe, kuti, “Palibe kalikonse ka mwa mwayi.” Mulungu anadziwa chirichonse. Ndipo basi izo sizinachitike kuti zichitike mwa njira iyo. Zinangokhala kuti Mulungu anazipanga izo mwa njira iyo.

<sup>31</sup> Ndiyeno pamene ife mmalingaliro athu aang'ono okhala ndi malire tiyamba kulingalirapo, “Chifukwa chiyani Mfumu yayikulu ya Kumwamba ikanasankha malo aang'ono ngati awo, mmalo mwa likulu?” Mmalo mwa ena . . .

<sup>32</sup> Ngakhale uko analipo malo ambiri amene anali nawo maziko auzimu aakulu kuposa omwe Betelehemu anali nawo. Mwa chitsanzo, malo ena ngati Silo. Silo anali malo opembedzera akale a Israeli, kumene iwo onse ankabwera chaka ndi chaka ku malo aakulu awa kumene likasa la Ambuye linkapumira. Ndipo nkudabwa bwanji, ndiye, kuti Iye sanakabadwire ku Silo?

<sup>33</sup> Ndiye kunali Giligala, malo ena auzimu aakulu opembedzerako. Chifukwa chiyani Mulungu sanamulole Iye kuti akabadwire ndiye ku Giligala?

<sup>34</sup> Ndipo uko kunali ena amodzi, Zioni. Zioni anali pamwamba pa phiri. Ndipo ife tikudabwa chifukwa chiyani kuti Yesu sanakabadwire ndiye mu Zioni, chifukwa iwo akhala chizindikiro chachikulu cha mbiriyakale a kumene Ambuye adalitsako anthu Ake mu mibadwo.

<sup>35</sup> Ndipo izo zikuwoneka ngati kuti mwina Iye akanasankha Zioni, kapena Giligala, kapena—kapena Silo, kapena amodzi mwa malo ena aakulu kumene kunali kutakhala madalitso aakulu ndi zophunzitsa zazikulu.

<sup>36</sup> Ndipo uko inalipo mizinda yina yayikulu, monga ngati Hebroni. Amenewo anali malo a munthu amene anali kufuna mzinda obisalako, malo a chitetezo. Uko kunali Ramoti-gileadi, nawonso, malo ena obisalako kumene anthu amakhoza

kubwera, chimene chikanakhala choyenera kwambiri kuti iye akabadwireko.

<sup>37</sup> Ndipo mwina, ngati ine ndikanamaganizira izo, ine ndikanadzamubweretsa Iye ku Kadesh-barnea pakuti uko kunali mpando wachiweruzo, ndi malo othawirako. Mwina ine ndikanadzamubweretsa Iye ku dziko ilo kukakhala malo obadwirako Ake, kapena mwina ife tikanadzasankha yina ya mizinda yina.

<sup>38</sup> Koma, inu mukudziwa, ine ndiri wokondwa kwambiri kuti ngakhale zinthu zazing'ono chabe zosalabadiridwa mu Baibulo zimatanthauza mochuluka kwambiri. Ine ndikukhulupirira kuti uyo anali Yesu amene ananena izi, kuti, “Inu mumalambalala, ndi kuchita zinthu zolemerera za lamulo,” kani, “koma mumalambalala pa zinthu zazing'ono.” Ndipo nthawi zina ndi zinthu zazing'ono zimene zimagwirizira zinthu zazikulu palimodzi. Koma, zonse mu zonse, magudumu aakulu akutembenezika chimodzimidzi basi mwa njira yomwe Mulungu anakonzera kuti iwo aziyitana... sipadzakhalala limodzi liti lidzaphonye malo ake. Mulungu wakonzera zinthu zonse, ndipo izo ziyenera kugunda chimodzimidzi basi ku malo amenewo.

<sup>39</sup> Ndipo pamene ife tipeza chikhulupiro chotere, ndi kuyamba kuganiza za, “Ndani ali kuseri kwa izi zonse? Ndi sipuring'i yaikulu iti imene ikutembenuza chuma chachikulu cha Mulungu ichi?” Ife tikupeza kuti ndiwo Mzimu Woyera. Sizinasiyidwe mmanja a munthu kuti achite zinthu; koma mmanja a Mzimu Woyera. Ndipo Iye ali sipuring'i yaikulu, kuti ngati Iye angakhoze kupeza zipangizo zonse, izo zidzagwira ntchito mwangwiro kumene ndi kusunga chimodzimidzi nthawi ya Mulungu.

<sup>40</sup> Ndiyeno ife tikuona izo ndipo ife tikudadwa mmalingaliro athu ndiye, pamene ife tiyang'ana pa zinthu zazikulu ndi momwe ife tikanadzakhallira nazo izo; ndiyeno chimatipatsa ife chithonhozo chochuluka lero kuganiza kuti, mwina ngati ife tiri gulu laling'ono la anthu, mwina ngati ife tiri osadziwika kwa dziko ndi kwa mipingo yayikulu ya zipembedo, komabe Mulungu amagwiritsa ntchito zinthu zazing'ono izo nthawizina.

<sup>41</sup> Pakuti zinalembedwanso m'Malemba, “Musawope, nkhosa zazing'ono, ndi chifuniro chabwino cha Atate anu kuti akupatseni inu Ufumu.” Ndi chithonhozo chotani, kuti, ine ndikudziwa izo motsimikiza basi monga Yesu anayenera kukabadwira mu Betelehemu wamng'ono, kotero zidzakhala nkhosa zazing'ono zimene Atate ati adzazipatse Ufumu, chifukwa izo zinalembedwa. Ndipo Malemba onse anapatsidwa mwa kudzoza, ndipo Malemba sangakhoze kuswedwa. Iwo ayenera kukwaniritsidwa. Kotero izo zikutipatsa ife chiyeembekezero icho, kudziwa kuti—kuti zidzakhala nkhosa

zazing'ono zimene ziti zidzalandire Ufumu, nkhoa zazing'ono zokhulupirika za okhulupirira. Ine ndikudalira kukhala imodzi mwa nkhoa zimenezo, kapena, mu nkhoa zazing'ono izo, ine ndiyenera kunena.

<sup>42</sup> Ndiyeno ife tikuyidziwa nkhani, ambiri a ife tikudziwa nkhani ya momwe Israeli anabwerera mu Palestina mwa lonjezo la Mulungu. Ndipo ife tikudziwa kuti Yoswa wamkulu uyo anali mmodzi amene anagawira fuko lirilonse gawo lawo.

<sup>43</sup> Ndipo ndizo, ndithudi, ngati ife tikanakhala nayo nthawi ya pafupi kuchokera tsopano mpaka sikisi koloko usiku uno, kuti tikhale kumene pa phunziro ili, kuzindanditsa zinthu izi, kuti tipeze tanthauzo lenileni la izo; limene, ife tiribe, pafupi makumi atatu okha, maminiti makumi anai. Kotero ife tiyenera kukantha nsonga zazitali zokha, kudalira kuti Mzimu Woyera, kwa inu owerenga Baibulo, udzayika zonse za izo mu mtima mwanu, pamene ife tikupitirira.

<sup>44</sup> Kodi inu mumadziwa kuti magawo awo, momwe Yoswa anawagawira iwo mu Palestina, anapatsidwa mwa kudzoza? Ndipo amayi a Chihebri awo a mbadwa izo, pamene mwana anali kubadwa ndipo iye mu ululu wa kusawutsika, kuti abale mwanayo, iye amalankhula malo omwewo amene mbadwa izo ziti zidzakhalepo ndi kudzakhala pa masiku otsiriza.

<sup>45</sup> Kulankhula za kudzoza, Baibulo ili liri lodzozedwa! Ziribe kanthu kaya mwapang'ono chotani, Lemba lirilonse laling'ono liri nacho chinthu chopambana chotero icho mu Kalata, mu—chithunzi chachikulu. Zonse za izo, onse—Mawu onse ali odzozedwa, ndipo pa amenewo pakupachikika mathero a miyoyo, pakuti ndiwo Mawu a Mulungu Wachisavundi ndi Wamuyaya.

<sup>46</sup> Ndipo ngakhale amayi awo, pamene mwana amabadwa iye analankhula liwu lawo, limawayika iwo pamalo amene iwo ati adzakhale mu dziko lolonjezedwa, mazana a zaka kenako. Ndipo Yoswa, posadziwa izo, komabe mwa kudzoza komweko anawakhazikitsa iwo chimodzimodzi pamene iwo anali poti adzakhale.

<sup>47</sup> Ndipo Yoswa, akugawaniza, anagawa gawo la Yuda. Ngati inu mudzazindikire pa mapu, ndizo. . .mwachirengedwe chakumadzulo chabe kwa chigwa cha nyanja, mailosi pang'ono kummwera kwa Yerusalemu, likulu. Ndipo pamene Yuda anali kutenga gawo lake, kapena gawo lake kani, mu dziko, dera lake, ife tikanalitcha ilo, ndi zachirendo, koma mzinda wawung'ono uwu sunatchulidwe nkomwe, Betelehemu. Komabe iwo unali pamenepo, chifukwa chakuti Abrahamu. . . Kapena, ine ndikukhulupirira anali Rabeka amene anayikidwa pa malo amenewo. Koma iwo uyenera kukhala mudzi wawung'ono chabe wa mtundu wina, chifukwa ngati inu muwerenga Yoswa 5, inu mudzapeza kuti inalipo mizinda yayikulu zana ndi khumi



ndi isanu pansi pa ulamuliro wa Yuda, kupatula midzi ndi matawoni aang'ono; mizinda zana ndi khumi ndi asanu, amene akutchulidwa. Ndipo mwina pamene iyo inagawanizidwa, kuti Betelehemu anali wamng'ono kwambiri, mwina chabe ka—kanyumba kakang'ono kapena ziwiri, sunatchulidwe nkomwe mu cholowa. Ndiyeno ife tikupeza kuti iwo sunafike podziwika kwenikweni. . .

<sup>48</sup> Mmodzi amene anawuyambitsa iwo anali mwana wamwamuna wa Kalebu, mwana wamwamuna wa Kalebu, amene dzina lake linali, Salma, ndipo iye anawuyambitsa iwo. Baibulo linati iye anali tate wa iwo, chimene chikutanthawuza kuti iye anali woyambitsa wa Betelehemu. Mwa kulankhula kwina, iye ayenera kuti anasunthira mmenemo nayambitsa malonda a mtundu wina, ndi zogulitsa, ndi malonda, ndi zina zotero, izo zinakulitsa iwo. Ndipo kenako ife tidzapeza kuti chifukwa chenicheni cha iwo, kuti malo onse anali kuchitira nsanje kachidutswa ka dziko kakang'ono aka; kamene kanali kumpoto, ndi kummawa, ndi masitso pang'ono cha kummwera, pa mpita uwo. Ndipo iwo unali wachonde kwambiri mwa yonse ya Palestina. Iwo unali ko—kolima chimanga ndi kolima tirigu, ndipo uko kunali minda ya azitona yayikulu, ndi zina zotero, pa iwo, mu gawo ilo la Betelehemu, kapena Palestina, mapeto a chigawo cha Yuda.

<sup>49</sup> Ndipo ife tikupeza kuti uko kunadzakhalanso kwawo kwa hule Rahabu. Pamene Israeli anali atadutsa mzere wa mmalire wa Mtsinje wa Yorodani, kulowa mu Palestina, ife tikuyidziwa nkhanu ya Rahabu hule. Tiyeni timuwone iye mmawa uno kwa maminiti pang'ono tsopano, ngati do—dona wamng'ono, mkazi wamng'ono wokongola amene tsoka lina mu moyo anakakamizidwamo, pokhala wachikunja, anakakamizidwa kulowa mmoyo umene iye anali kukhala. Ndipo nthawi zambiri anthu amakakamizidwa mu moyo umene iwo amakhala.

<sup>50</sup> Ine ndinali mu ndende usiku wina, kumuona munthu amene anali kutenga chiweruzo. Ndipo ine—ine ndinamugwira iye pa dzanja, ndi kulankhula kwa iye. Ndipo ine ndinati, “Iwe ungachitirenji chinthu chotero ngati icho?” Ndipo atandigwira ine pa dzanja, iye anayamba kulankhula. Ndipo iye anakakamizidwa mu chimene iye anali kuchita. Ine ndinati, “Chifukwa chakuti iwe unalolera kuti icho chikukakamizire iwe kwa icho. Iwe suyenera kuchita icho. Iwe, palibe munthu amene ayenera kumwa.” Ine ndinati, “Ndine wamanjenje, inemwini, koma palibe chifukwa cha izo.”

<sup>51</sup> Ndipo mkazi wamng'ono uyu, atatha kumva kwake koyamba kwa Israeli, ndi kwa Mulungu amene anali m—Mulungu amene amakuyankha pemphero; osati kokha Mulungu koti nkupempherako, koma Mulungu amene amakuyankha; pamene iye anamva kuti panali Mulungu wa zozizwitsa, Amene akanakhoza kuchita zozizwitsa, Amene anawumitsa nyanja

ndi kuvumbitsa mkate kuchokera mmiyamba, mtima wake unayamba kunjenjemera. Ndipo pamene iye analandira uthenga woyamba kuchokera kwa alaliki awiri amene anapitako, mwamsanga iye anavomereza izo ndi mtima wake wonse. Ndipo panali chingwe chofiira chimene chinamangidwa pa zenera lake, kwa chitetezero cha nyumba yake, chifukwa chakuti iye anali atalandira uthenga.

<sup>52</sup> Ndipo ine ndikhoza kuwonjezera apa, kodi inu mukudziwa kuti iye ankayimira Mpingo wa Amitundu? Iye anali wa Amitundu, ndipo iye anali choyimira cha Mpingo wa Amitundu, pamene iwo anamva uthenga. Ife tinali tonse kunja mu chiwerewere chazimu, tikuchita ziweregere zauzimu motsutsana naye Mulungu Wakumwamba, mu mitundu yonse ya zinthu, mitundu yonse ya mipingo ndi zipembedzo. Koma pamene ife tinamva kuti panali Mulungu amene amakhalabe moyo, amene akhoza kuchita zozizwitsa, mwamsanga ife tinalandira Uthenga.

<sup>53</sup> Ndipo apo panayikidwa Magazi a Ambuye Yesu, amene anapanga chingwe chofiira. Ndipo kuti tisapite mwatsanetsatane, inu mukudziwa momwe iye anachipachikira icho kuchokera pa zenera lake, powonekera, Magazi anawonetseredwa poyera. Ndimomwe Magazi ayenera kuwonetseredwa, poyera atapachikika kuchokera panja pa khoma; kusonyeza kuti, mkati, chinachake chinali chitachitika. Ndimomwe wokhulupirira woona mwa Khristu aliri mmawa uno; kunjako kuli kuwonetsera kwa Magazi a Ambuye Yesu, izo zikusonyeza kuti chinachake chinachitika mkati.

<sup>54</sup> Ndipo kupyolera mu izi, Mulungu anayang'ana pansi pamene mkwiyo unagwa ndipo malipenga anayamba kuwomba, Mulungu anawona chingwe chofiira icho chitapachikika apo ngati chikumbutso. Nthawizonse zamukondweretsa Iye kudutsa pa Mwazi. “Pamene Ine ndiwona Mwazi, Ine ndidzadutsa pa inu.” Iye anawuwona iwo. Ndipo pamene kugwedeza ndi Mzimu Woyera unagwedula dziko lapansi ndi kugwedezera pansi makoma awo, mapazi ena makumi awiri kunenepa, palibe mwala umodzi umene unagwera pamene chingwe icho chinali kulendewera. Kusonyeza chitetezero cha Mulungu woona kwa wokhulupirira woona, ziribe kanthu ndi mchikhalidwe chotani chimene inu mulimo pamene Iye akupezani inu, ngati inu mudzangovomereza chingwe chofiira icho. Icho chimalukana kupyola m’Baibulo.

<sup>55</sup> Ndiyeno ife tikumuwona iye pamene iye anatengedwera mkati ngati mmodzi wa Aisraeli. Iye anakondana naye mwamuna, amene anali kapitao ndi kalonga mu Yuda. Iye anali kapitao wa ankhondo a Israeli. Dzina lake linali Salimoni, monga ngati mfumu, Solomoni. Ndipo iye anali kapitao, ndipo iye anakhala mu chikondi chachikulu ndi kapitao uyu, yemwe

anali kalonga wa Yuda. Ndipo potsiriza iye anakwatiwa ndi iye. Ndipo pamene chuma chinakhazikitsidwa kwa Aisraeli, iye ndi mwamuna wake wokondedwa ankakhala mu Betelehemu.

<sup>56</sup> Tsopano inu mwayamba kuziwona izo zikutseguka, sichoncho inu? Mwaona? Izo zikuyamba kutseguka pamene ife tikuona kuti mu Betelehemu iye ankakhala, pokhala mkwatibwi wa Amitundu, kwa Myuda. Chifukwa? Chifukwa iye anakhulupirira mwa Mulungu wochita-zozizwitsa. Ndipo mwa kuyang'ana kumene iye anachokerako, kuchokera pakukhala wochokera mnyumba ya mbiri yoyipa, ya uchiwerewere; kupyolera mu kutembenuka kwake ndi kupyolera mu chikhulupiriro chake chosalephera mwa Mulungu, izo zinamuchotsa iye kuchokera ku nyumba ya uchiwerewere, kupita ku nyumba yokongola mu Betelehemu. Nkusiyana kotani!

<sup>57</sup> Ndimo momwe izo zimatichitira ife tonse. Kuchokera ku nyumba ya kusakhulupirira ndi zokhumudwitsa, machitidwe oyipa awo, ndi chirichonse; kupita ku malo, okhazikitsidwa mwa Khristu, chimene chiri chokongola kwambiri. Kuchokera ku chotonzedwa kupita ku chapamwamba, ndiko kusiyana kumene izo zimapanga kupyolera mu kutembenuka kwathu. Ndipo kodi inu munaona, iye anakwatiwa ndi kalonga wa nyumba ya Yuda, kapitao? Kapitao uyo ankayimira Khristu, anadzitengera kwa Iyemwini Mkwatibwi wa Amitundu. Kuchokera ku chotsika cha chotsikitsitsa, kupita ku chachikulu ndi malo abwino mu dziko, monga ife tidzafike ku izo kenako mu Uthenga wathu, kutsimikizira kuti sichinali chinanso chimene chikanakhoza kukhala koma icho. Iwo ali choyimira cha Mpingo wa Amitundu.

<sup>58</sup> Ndipo ife tikupeza kuti iwo anali nayo nyumba yokongola mu Betelehemu, monga Salimoni anali—anali atawayambitsa iwo, ndipo iwo akanadzakhala malo aakulu, ndi nthaka zachonde. Ndipo momwe ziriri zokongola kuganiza za dziko la tirigu ilo uko, kuti awo akanakhala malo a mkate wa mdziko. Ndipo, izo nzoona, nzosadabwitsa Yesu amayenera kukabadwira kumeneko, chifukwa Iye anali Mkate wa Moyo! Uko ndi kumene mafuko onse amadzera tirigu wawo, fuko lonse limadzera chimanga chawo. Pakuti, munali mu Betelehemu, mmene anali nazo nthaka zachonde izo. Ndipo, inu mukuona, kanthu kakang'ono kwambiri, kunena chabe, “O, chinali chigawo cha tirigu,” komabe icho chimatanthawuza chinachake. Ndipo inu mukuona momwe kalonga wa Amitundu, kapena kalonga wa Chiyuda uyu akutenga mkwatibwi wake wa Amitundu kubwerera ku Betelehemu, ku malo okakhazikikako, malo oti akakhaleko, kumene kunali mkate wochuluka.

<sup>59</sup> Ife tikupeza, kupyolera mu chikondi chachikulu ichi ndi kumvera kwakukulu ku chikhulupiriro, kupyolera mu Rahabu hule, iye anabala mwana wamwamuna kwa Salimoni, ndipo

dzina lake linali Boazi. Ndipo ife tonse tikuyidziwa nkhani yina yayikulu yomangiriza mu kufanana uku apa tsopano. Ndipo Boazi anabadwira mu Betelehemu, kuchokera kwa Salimoni ndi Rahabu hule.

<sup>60</sup> Ndipo ndife... tikupeza kuti zaka zotsatira, atatha Naomi kuchoka mdzikolo ndi kupita kukayenda ndi Amoabu, ndipo pamene iwo anali moyipa anali atamuzunza iye ndipo anali atasiyana nawo chiyanjano okhulupirira onse, nadziyanjanitsa yekha mu chikhalidwe chakugwa, mu dziko lina, pakati pa anthu ena. Mwa njira yina, iye anali atawusiya Mpingo wokhulupirira moona, kupita kunjā mu dziko kwa kanthawi pang’ono, kukalumikizana nawo mpingo wina wachidziko, umene unakhulupirira mu chirichonse basi chimene chikanakhala cholondola. Kumeneko, iye anataya mwamuna wake.

<sup>61</sup> Ndipo izo sizisowa nthawi zonse kukhala mu imfa yathupi. Inu mukhoza kumutaya iye mu imfa yauzimu, kapena kumutaya mkazi wanu. Kulibwino mukhale pa malo abwino! Inu kulibwino mukhale kumene inu mukudziwa kuti inu mwaphimbidwa ndi Magazi, mopanda kusamala chimene ena onse amawoneka ngati, momwe iwo aliri aakulu, kaya ali ndi zazitali zabwino chotani pa matchalitchi awo, kapena momwe mabelu aakulu amalirira. Kulibwino inu mukhale kumene Magazi akuphimba machimo a anthu. Inu mukhoza kutayana wina ndi mzake, ndipo, pamwamba pa zonse, inu mukhoza kuwataya Ambuye Yesu ndi kutsekeredwa kunjā.

<sup>62</sup> Ndipo ife tikupeza ndiye kuti atatha ana ake kupita, iye anali atawataya onse a iwo, ndipo iye anabwerera mmbuyo chifukwa uko kunalibe mzimu wa chitsitsimutso mu mzinda, pa nthawiyo.

<sup>63</sup> O, momwe ine ndikanakondera kupumula apa kwa maminiti pang’ono! Momwe ine ndikufunira kutengera izo pomwe pano ndi kukuwonetsani inu! Mosalabadira za kuchuluka kwa mipingo yomwe yapita mmbuyo; khalani pansi pa Magazi, ndiwo malo woti mukhalepo. Mkati kapena kunjā, pamwamba kapena pansi, wonenepa kapena owonda, kulikonse kumene iwo angakhale, khalani pansi pa Magazi. Koma Naomi, iye ankaganiza kuti icho chidzakhala chabwino kupitako ndi kukajowina gulu lina, chifukwa iwo anali ndi mavuto, mkate wauzimu—mkate kunalibe uko. Ndipo, koma Mulungu adzabwezeretsanso iwo, “Ine ndidzabwezeretsa, atero Ambuye.” Khalani mmunda kumene Iwo umachokerako.

<sup>64</sup> Kotero ife tikupeza kuti iye anayamba kufuna kubwerera, chifukwa iwo anamva kuti chitsitsimutso chachikulu chinali chitayamba. Ndipo ngati inu munazindikira, Naomi anabwerera mu “nyengo ya barele,” Baibulo linatero, pa nthawi kumene ya kukolola; mwa kulankhula kwina, pamene uko kunali chitsitsimutso chachikulu chikuchitika, kuyika izo mwauzimu.

Iye anabwerera kumene mu nyengo iyo. Palibe chinatsalira; iye analibe kanthu.

<sup>65</sup> Ndipo Olipa, mmodzi wa akazi a ana ake aamuna, pamene iye anabwera kuti adzawone pa chimene iye ayenera kupereka nsembe, pokhala choyimira cha mpingo wamakono, “Ngati ine nditi ndipite uko, ine ndidzayenera kuchoka ku zovina zanga, ine ndidzayenera kuchoka ku nthawi yanga yayikulu, ndi kusunkhana kwanga kodyerera.” Ndiye iye anangolira ndi kuwapsyopsyona apongozi ake aakazi, nabwerera mmbuyo.

<sup>66</sup> Koma apa pali chithunzi chokongola, analipo mmodzi dzina lake Rute, ndi iye, mpongozi winanso wamakazi, chimene chinali choyimira kachiwiri cha Mkwatibwi wa Amitundu, amene anawapsyopsyona apongozi ake aakazi, nanena, “Ine ndidzasiya chirichonse. Ine ndikupita nanu inu. Mulole anthu anu akakhale anthu anga. Mulole Mulungu wanu akakhale Mulungu wanga. Kulikonse kumene inu mukafere, uko ine ndikaferako. Kumene inu mukayikidwe, uko ine ndikayikidwako.” Ndi zimenezo. Ndicho chimene Mulungu akufuna. Siziri za mmalire, zatheka; koma mtheradi, kudzipereka kwathunthu ku Ufumu wa Mulungu. Iye anamupsyopsyona iye.

<sup>67</sup> Ndipo kotero Naomi anati, kufuna kumukhumudwitsa iye, anati, “Kulibwino iwe ubwerere kwa anthu ako. Ine ndine wokalamba, ndipo mulibenso ana ena aamuna mwa ine.” Ndipo lamulo linali lakuti iye amayenera kuyembekezera mwana wamwamuna. Ndipo anati, “Ndiye mulibenso ena mwa ine. Ndipo ngati ine ndikanadzakhala naye mwamuna, ndipo nkukhala naye mwana wamwamuna, iwe ukanadzakhala wamkulu kwambiri kuti ukwatirane naye iye, kotero iwe ungobwerera kwa anthu ako.”

<sup>68</sup> Koma Rute anati, “Ine sindibwerera!” Chikhulupiro, chinazikika, chinakhazikika, chikhulupiro changwiwo chinali chitadza mu mtima wa Rute. Iye anati, “Ine ndikupita nanu kumene inu.” Ndipo iye anakangamira kwa iye, anagwiritsitsa kwa iye. “Ine ndikakhala kumene inu muti mukakhale.” Ine ndimakonda zimenezo.

<sup>69</sup> Ndipo ife tikuyidziwa nkhaniyi pamene iyo ikupitirira, kuti Boazi wamkulu uyu, amene anali mbuye wa zokolola, anali mu zokolola pa nthawiyo, ndipo anali wachibale kwa Naomi. Ndipo pamene iye anampeza Rute kunjwa uko mu kamishoni kakang'ono, akukunkha, tsache lililonse laling'ono limene iye akanakhoza kutola, limene linali ndi tirigu pa ilo, iye anagwiritsitsa kwa ilo, pakuti linali moyo. Boazi, pokhala mbuye wa zokolola, iye analamulira kuti okolola ake azimugwetsera iye zodzaza dzanja pafupi ndi pafupi, za iye; ndipo iye amatola izo, ndi chisangalalo. Ndiyeno iye amapuntha mosamala kwakukulu kwa iwo, tsiku limenelo. Ndipo pamene

Boazi, mbuye wa zokolola, anatulukira nayang'ana pa Rute, ndi kuwona kukhulupirika kwache, iye anamukonda iye.

<sup>70</sup> Taonani Boazi akuyimira Khristu. Kodi iye anali kuti? Betelehemu. Kodi Rute anabwera kuti? Betelehemu. Kodi iye anali kukunkha kuti? Mu Betelehemu. Mukuona matanthawuzo onse auzimu mpaka ku ichi apa, maziko ku chowonekera chachikulu ichi chimene chikuchitika, Mulungu kudziwa izo pachiyambi?

<sup>71</sup> Ndipo iye anayamba kumufunsa mpongozi wake wamkazi, chimene iye ayenera kuchita. Ndipo potsiriza Rute anakwatiwa kwa Boazi, Wamitundu kukwatiwa kwa kalonga kachiwiri, mu Yuda, nakhazikika pansi ndi kukhala mu Betelehemu.

O, iwe Betelehemu wamng'ono, kodi suli iwe wochepesetsa pakati pa mizinda ikuluikulu ya—ya Palestina; koma izo zinamukondweretsa Mulungu, Amene kudziwa kwake ndi kupita kwake kunali kuchokera kwakale, kuchokera pachiyambi, kuti Mwana Wake wamwamuna akabadwire kumeneko.

<sup>72</sup> Iye amadziwa zinthu zonse, ndipo Iye amachita izo kuti zikhale molondola basi. Ndipo uko Rute anakwatiwa ndi Boazi. Ndipo pamene Rute ndi Boazi anakwatirana; ngati ife tikanakhala nayo nthawi kuti tilowe mu nkhani yayikulu uko, imene inali imodzi mwa kuwonekera kwakukulu kwa chikondi cha mibadwo yonse, pamene Rute ndi Boazi anakwatirana. Ndipo kumbukirani . . .

Tiyeni tingoyima kwa miniti apa. Zabwino kwambiri kuti tizilambalale!

<sup>73</sup> Rute anali wa Amitundu. Iye analibe cholowa nawo Ayuda, monga ngati ife Amitundu tinalibe cholowa. Kotero Naomi anali makamaka mmodzi woti atenge cholowa. Kotero iye anali atataya munda wake woyamba, katundu wake yense anali atagulitsidwa pa okishone ya onse, choncho iye anali . . . anali atachotsedwa, ndipo anali atapita kutali.

<sup>74</sup> Tsopano pamene iye anabwerera, uko kunali munthu mmodzi yekha amene akanakhoza konse kuwombola cholowa chake chotayika, ameneyo anali wachibale wapafupi kumene kwa iye. Ndipo Boazi anadziwa izi, kotero iye ankanenera kugwira ntchito mwa njira yina kuti amutenge msungwana wa Amitundu uyu akhale mkazi wake. Ndipo kodi iye amayenera kuchita chiyani? Iye amayenera kugula minda yonse ya Naomi, ncholinga chakuti apeze chuma ichi, chimene Rute anali gawo la chuma cha Naomi. Ndipo munthu yekhayo amene akanakhoza kugula icho, amayenera kukhala munthu amene anali wachibale, wachibale wapafupi. Ilo linali lamulo la chiwombolo.

<sup>75</sup> Ndipo njira yokhayo imene Khristu akanakhoza konse kugulira chuma cha Israeli wobwerera mmbuyo, inali kukhala

Wachibale. Njira yokhayo imene Mulungu akanakhoza kuwombolera mtundu wa anthu, Mulungu Mwiniwake ankayenera kupangidwa thupi. Ndipo Yesu anali Mulungu wopangidwa wachibale kwa mtundu wa anthu. Iye anali Emanuele. Iye anakhala wachibale. Iye sanadzitengere pa Iye mawonekedwe a Angelo, koma mawonekedwe a wantchito amene ankatsuka mapazi nakhala moyo. Ndipo nkhandwe zinali nawo maenje, ndi mbalame za mlengalenga zinali nazo zisa, koma Iye analibe ngakhale malo kuti ayikepo mutu Wake. Iye ankadya, Iye ankamwa, Iye—Iye ankalaria, Iye ankaseka, monga ngati munthu wina. Ndipo Iye anali Mulungu, osati mneneri. Iye anali Mulungu, chifukwa Iye ankayenera kukhala wachibale kuti awombole mtundu wa anthu wotayika. Kotero, Boazi, mu choyimira chachikulu ichi ku Betelehemu; taonani kumene Wachibale uyu anabadwirako kwa mtundu wa anthu, ankayenera kutero.

<sup>76</sup> Ndiyeno pamene Boazi wamkulu uyu anamuwombola iye, iye ankayenera kuwonetsera poyera kuti iye anali atawombola chuma chake chonse chotayika. Kotero iye anapita ku chipata cha Betelehemu, mzinda wawung'ono uwo kachiwiri, ndipo iye anayitanitsa akuluakulu a mzinda, ndipo iye anawalola iwo kudziwa kuti tsiku limenelo iye anali atagula chirichonse chimene chinali. . . Naomi anali atataya. Chirichonse chimene iye anataya, iye anagulanso icho. Ndipo iye anavula nsapato yake nayiponyera iyo pamaso pa anthu, ngati chizindikiro, “Ndipo ngati alipo aliyense amene ali nacho chifukwa chirichonse kuti anene chinachake, anene icho tsopano, pakuti ichi ndi chikumbutso kuti ine ndawombola chirichonse chimene iye anataya.”

<sup>77</sup> O, lidalitsike Dzina la Ambuye! Ndipo pamene Wachibale wathu anabwera, Yesu wa ku Nazareti, wobadwira mu Betelehemu, Iye anayima pamwamba pa Gologota, ndipo anamukweza Iye pamwamba pa Miyamba ndi dziko lapansi, ngati chikumbutso kuti Iye anali atawombola chirichonse chimene mtundu wa anthu unali utataya mu kugwa. Munthu angakhoze bwanji kunyoza machiritso Auzimu ndi mphamvu za chiwukitsiro cha Ambuye Yesu, pamene chizindikiro cha poyera chinapangidwa pa Kalvari, kuti, “Ine ndawombola mtundu wonse wa anthu ndi chirichonse chimene iwo anataya konse,” anawombola moyo wathu, anawombola thupi lathu, anawombola chirichonse chimene ife tinachitaya mu kugwa. Wowombola wathu Wachibale anadza ndipo anapangidwa thupi, nakhala pakati pathu, ndipo anapereka chizindikiro, ndi kunena, “Kwatha.” Chathacho chiyani? Chirichonse chatha. Ife tikuyenda basi kulowa mu cholowa chathu. Ndipo pamene masiku akupitabe, ife tikuyenda pafupi ndi pafupi.

<sup>78</sup> Boazi ndi Naomi. . . Atatha kukwatirana kwa nthawi yina, iwo anabala mwana wamwamuna, yemwe anawonjezera

mochuluka ku mzera wa m'badwo, ndipo ameneyo anali Obedi. Ndipo iye nayenso anabala mwana wake wamwamuna, amene anali Jese. Ndipo Jese anali nawo anyamata asanu ndi atatu.

<sup>79</sup> Ndipo anali mneneri wamkulu Samueli amene anabwera nayo nsupa ya mafuta, mneneri wamkulu amene anapita kwa Jese, nanena, “Mulungu wasankha mmodzi wa anyamata ako kuti alamulire ndi kutumikira anthu Anga.” Ndipo iye anali kunja kuseri kwa munda, mu malo aang'ono a m'busa, kumene mnyamata wamng'ono wofiira magazi, wosakhwima-mmawonekedwe anabweretsedwa, Davide, wakale... wamng'ono kwambiri. Ndipo Samuele anatsanulira mafuta odzozera pa iye, mu kukhalapo kwa abale ake onse ndi iwo amene anayima pozungulira, natsimikizira kuti Mulungu anali atamudzoza iye kukhala mfumu. Ziri kuti izo? Betelehemu. Ulemerero kwa Mulungu mMwambamwamba! Nzosadabwitsa, Betelehemu, kumene iye anadzozedwera kukhala mfumu.

<sup>80</sup> Ndipo munali mu Betelehemu, kumene Davide anabadwirako. Ndipo Mwana wake wamwamuna wamkulu, Yesu, anali nayenso woti akabadwire mu Betelehemu, chifukwa pali kulukana kwapafupi pakati pa awiriwa, monga Atate ndi Mwana. Sanali kokha Mwana wamwamuna wamkulu uyu Mwana wamwamuna yekha, Iye anali Muzu ndi Mphukira ya Davide, Iye anali ngakhale asanakhale Davide, Iye adzakhlapo patsogolo pa Davide, Iye analipo kwa nthawizosatha, kuchokera ku nthawizosatha mpakana. Koma molingana ndi thupi, ndi zinthu zonse zoti zikwaniritsidwe, Iye anali Mwana wa Davide. Iye anali woti abadwa zaka zotsatira mu Betelehemu yemweyu, mzinda wawung'ono wosiyidwa uwu.

<sup>81</sup> Koma nthawi yonse, mmenemo, kodi inu mukuzindikira, pakuchitika chinsinsi chachikulu champhamvu mwakuti palibe mmodzi ankawoneka kuti akumvetsa. Ndicho chinthu chomwe chimene chiripo mu Betelehemu wa Mulungu lero, pakuchitika—chizindikiro chachinsinsi, koma palibe mmodzi amene akuwoneka kuti akumvetsa izo. Ndicho chinachake chimene chikudutsa pamwamba pa mitu ya anthu. Iwo sakuwoneka ngati akumvetsa izo. Ziribe kanthu zimene zachitika, kapena zimene zanededwa, ndi gawo lachinsinsi la zinthu zimene zachitidwa, anthu amayang'ana kunena, “O chabwino, ine ndikuganiza ziribwino,” ndikumapitirira, koma iwo samamvetsa izo. Iwo sangakhoze kumvetsa izo. Iwo sangakhoze kugwira izo. Ndipo ndicho chimene Mulungu anali kuchita mu Betelehemu mu Yuda. Iye akuchita, zinthu zonse zazing'ono izi kuti zizisunthira mmwamba, kuti zidze ku mutu umodzi wawukulu.

<sup>82</sup> Davide, o, pamene iye anadzozedwa kukhala mfumu, ngati m—mnyamata wamng'ono, iye anali wosakhwima pomuyang'ana, koma iye ayenera kuti chinachake mwa iye chinkawoneka chenicheni kwa Mulungu. Wamng'ono



kwambiri, wamng'ono kwambiri wa banjalo. Anyamata onse, anthu wamphamvu wamkulu wabwino, akhoza kuwoneka bwino mmikanjo, ndi korona pa mutu wawo. Koma Mulungu anasonyeza chimene Iye amayang'anapo; osati pa mawonekedwe akunja, koma mkati mwa munthu. Iye anayang'ana pa mtima wake, ndipo Iye anadziwa chimene chinali mu mtima wa Davide, zinalibe kanthu kaya koronayo amawoneka bwanji pa iye. Iye anadziwa kuti Iye anali kumupezera Iye munthu amene anali munthu wapamtima Pake Pomwe, chimene Davide akanakhala munthu wapamtima Pake Pomwe. Ndicho chifukwa Iye anatsanulira mafuta odzodzera, kapena anatsanulira iwo pa Davide. Chimene, dzina lakuti *Davide* limatanthawuza “wokondedwa.”

<sup>83</sup> Ndipo izo zinayimiridwa bwino mwa Yesu, Mmodzi Wokondedwayo, zaka zotsatira; Mwana wa Davide, Yemwe anali kudza kudzakwaniritsa zinthu zonse zimene zinali zitalonjezedwa. Mzinda wawung'ono uwu wa Betelehemu unali kumene izi zinachitikira. Ndipo anali pa mapiri omwewo aang'ono a Yudea kumene Davide anali atakalishyako nkhoa zake, zaka zambiri zotsatira, kuti Angelo anayimba nyimbo yawo yakubadwa yoyamba pa mapiri a Yudea, akuyang'ana pa Betelehemu. Nyimbo yoyamba yakubadwa, “Kwa Inu kwabadwa mu mzinda wa Davide, Khristu Ambuye.” Pamene Angelo poyamba anapanga kuwonekera kwawo koyamba kuti ayimbe, sikunali ku Yerusalemu, mpingo wawukulu; ngakhale kuti kunali ku Giligala; kapena kuti kunali ku Silo, kumene iwo ankakhala ndi kupembedza kwa chipembedzo cha mpingo nthawi yonse. Koma munali mu Betelehemu wamng'ono, kumene Mzimu wa Mulungu unali ukusuntha mwa njira yachinsinsi, kubala chinachake. Kunali kumeneko.

<sup>84</sup> Kunali uko kumene Khristu ankayenera kubwera. Kunali uko. Munali kumene mu Mzinda wawung'ono uwo, ndi Mfumu kukabadwirako, mayi uyo, namwali, anabala mwana wake wamwamuna woyamba kubadwa. Anatezeza, ndi kuyikidwa mu chotchinga chake chaching'ono, Mfumu ya mafumu ndi Ambuye wa mbuye. Kumene sanali Samuele yekhe amene anabwera kudzatsanulira mafuta odzozera, koma Mulungu anatsanulira pa Iye, ndi pa dziko, Khristu Ambuye. Angelo anatsogolera kudza Kwake nayimba kwa abusa pa mbali ya phiri, amene anatsatira Davide mfumu, zaka mmbuyo. Mukuona chinsinsi cha Mulungu, momwe icho chiriri chachikulu?

<sup>85</sup> Iye anabadwira mu malo aakulu a tirigu awa, amene tirigu amadzakhala maziko a zolinga za moyo. Ndipo Iye anali Mkate wa Moyo. “Ine ndine Mkate wa Moyo. Iye amene adya thupi Langa namwa Magazi Anga ali nawo Moyo Wamuyaya, ndipo sadzafa konse kapena kubwera mu kutsutsidwa, koma wadutsa kuchokera ku imfa mpaka ku Moyo.”

86 Betelehemu! Dzina lakuti beth-el. B-e-t-h, beth, *beth* mu mawu a Chihebri limatanthauza “nyumba.” *E-l* amayimira Elohim, mwachidule mwake, *Elohim* amatanthauza “Mulungu.” B-e-t-h, beth; E-l, E-l ndi Elohim, amene ali Mulungu, Nyumba ya Mulungu, kumene Mkate wa Moyo wayikidwako. E-l, h-e-m, tsirizani izo ndipo mubweretsenso l wanu ndi e wanu, kutanthawuza “mtanda wa mkate,” mu Chihebri, El-hem. E-l ndi Mulungu, Elohim. B-e-t-h ndi mkate, kapena b-e-t-h ndi. . . b-e-t-h ndi “nyumba.” E-l, ndiye Elohim, mwachidule mwake. Ndiye E-l, he-m ndi “mkate.” Iye ndi ndani? Nyumba ya Mkate wa Mulungu. “Nyumba ya Mkate wa Mulungu.” Nyumba, *beth; Elohim*, Mulungu; *El-he-m*, mkate. “Mkate wa nyumba ya Mulungu,” kutanthauza Betelehemu.

87 Ndikuti kumene Iye akanakhoza kukabadwirako kwina kulikonse koposa uko? Koma izo zinabisidwa kwa aliyense kupatula mneneri uyo; iye anati, “Kuchokera mu Betelehemu adzabwera Iye.” Iwo anali kuyang’ana mu Yerusalemu; iwo anali kuyang’ana mu Silo wamkulu yense; iwo anali akuyang’ana kulikonse. Koma Iye anabwera kuchokera ku Betelehemu, chifukwa iyo inali Nyumba ya Mkate Wamoyo wa Mulungu. Iye ali dengula iyo inali Nyumba ya Mulungu kwa dziko. Uko Iye anali, anabadwira mu Betelehemu. Iye sakanakhoza kubadwira kwina kulikonseko.

88 Uko kukanakhoza kukhala zinthu zazikulu zambiri, zimene ine ndinali kuwerenga sabata ino za mawonekedwe auzimu osiyana kwa izo, chifukwa chiyani Iye ayenera kubadwira mu Betelehemu. Pamene ine ndinagunda malo pang’ono awa, Mzimu Woyera unangonditengera ine kutali, ndipo ine ndinati, “O Mulungu, izo nzokwanira. Ine ndikuona izo tsopano.”

89 Iye sakanakhoza kubadwira kwina kulikonse koma ku Betelehemu. Iwo anali malo a mkate wa fuko. Iwo anali mkate wa nyumba yonse ya Israeli, wobwera kuchokera kumeneko. Ndipo Iye anali Mkate wa Moyo umene unabwera pansu kuchokera Kumwamba, Manna auzimu; ayenera kubwera kuchokera ku Betelehemu, mzera wa mkate, kumalo kumene mkate umakhalako. Betelehemu, kuphika kwa mkate. Tsopano, Yesu pokhala Mkate wa Moyo, “Munthu akhoza kudya za iwo,” Iye anati, “ndipo sadzafa.”

90 Chochitika china chachikulu chimene ine sindingayiwale kukumbukira, apo panali pamene Davide anali mu nthawi yake yovutitsitsa, pamene iye anali wobisala. Iye anali atadzozedwa kale, iye ankadziwa chimene iye ankayenera kukhala. Iye anali woti akhale mfumu, Mulungu ananena choncho, ndipo komabe iye ankadanidwa. Iye anali kuyima pakati pa moto uwiri wakuya; apa panali Afilisti kumbali imodzi, pambuyo pake, apa panali Saulo ku mbali yina. Ndipo iye anali munthu wopanda fuko.

<sup>91</sup> Basi monga Mpingo ukuyimira lero, Mpingo woona wamoyo wa Mulungu, wopanda chipembedzo kapena china chirichonse. Iwo ukuyima wokha, komabe Iwo wakhala nako kudzoza kutatsanuliridwa pa Iwo. Iwo ukudziwa chimene Iwo uli.

<sup>92</sup> Zingakhoze chotani mu dziko kukwaniritsidwa, Mdierekezi ku mbali zonse, akulondolera pa Davide? Iye anali atathawira mu malo amphamvu mu nkhalango ndi mu mphanga, kuyesera kukabisala, ndi gulu laling'ono la ankhondo okhulupirika, apang'ono chabe akukhulupirira monga iye. Koma amuna awo anakhulupirira Mulungu, kuti uyo adzakhala mfumu.

<sup>93</sup> Kotero ali okhulupirira lero, amene abisala kuchokera pa malo kumka ku malo, komabe iwo akudziwa Yemwe akubwera kuti adzakhale Mfumu. Ine sindikusamala za yemwe ati akhale Purezidenti. Ife tikudziwa Iye akubwera. Ndipo iyo imayang'ana kutali kuposa momwe izo zinachitira konse, pamene sayansi ikuyesera kulamulira mopitirira, ndi kunena, "Iwo akhoza kumumanga munthu, iwo akhoza kuchita *ichi*, ndipo iwo akutenga mbira ndi kutenga umuna ndi kupanga mbira yina, ndi zinazotere," kuyesera kutsutsa Mawu a Mulungu. Komabe, pali anthu amene amakhulupirira Mulungu, amene amangoyima okonzeka monga iwo amachitira nthawizonse. Ziribe kanthu zimene ziti zibwere kapena zipite, iwo amakhulupirirabe Mulungu. Mulungu akulondola! Iwo amagwira ku manja osasintha a Mulungu. Mkati mwa nkondo, mkati mwa misonzi, mkati mwa matenda ndi imfa, ndi chirichonse, iwo amagwirabe ku dzanja losasintha la Mulungu. Iwo akudziwa kuti Iye ali Mfumu yomwe ikudza.

<sup>94</sup> Anthu lero amaseka ndi kuwatonza iwo, ndi kuwacha iwo, "oyera-odzigudubuza," kuwacha iwo chirichonse chimene iwo akufuna kuchita, koma ankhondo awo a Mulungu amayima mokhulupirika pa malo antchito. Akhoza kuwacha iwo "gulu lochiritsa," inu mukhoza kuwacha iwo "gulu la otentheka," kapena chirichonse chimene inu mukufuna; iwo amakanirira kwa Mfumu iyo. Iwo amadziwa kuti Iye akubwera mu mphamvu. Ngakhale iwo atatenga Dzina Lake pachabe, kunyoza ndi kutonza, kuwacha anthu amene amakhulupirira Iye, "otayidwa, gulu la mngalande," izo sizimawakhudza iwo pang'ono, iwo amakhala owona pa malo antchito.

<sup>95</sup> Ankhondo awo amene anali ndi Davide, anakhala naye pambali yake. Ngati Mfilisti abwera, iye amayenera kumenya. Aliyense amene analipo, iwo ankgonjetsedwa, mbali iliyonse. Davide wosauka, mu dzanja lake, yense wosokonezedwa; iye anaganiza, "Zingakhoze kukhala chotani izo, Ambuye?"

<sup>96</sup> Inu mukudziwa, atsogoleri nthawizina amapyola mu zinthu zimene osonkhana samadziwa zimene iwo akupyolamo. Pamene iwe uganiza za malonjezo amene Mulungu wawapanga, ndiye bwanji izo sizikukwaniritsidwa? Iwo samawuza osonkhana awo,

iwo samawawuza anthu omwe iwo amayanjana nawo, koma pali zokhumudwitsa zambiri mu mtima wa mtsogoleri weniweni.

<sup>97</sup> Davide atakhala pamenepo, kwake—ku mmero kwake kukutentha, ndipo panali pakati pa chirimwe. Afilisti anali kupezera mwayi wa kugawanikana uko pakati pa Davide ndi Saulo. Ndipo Saulo akufunafuna Davide kulikonse, ndi Afilisti, nawonso, ndiyeno Afilisti akufunafuna Aisraeli. Kunena za nthawi ya chisokonezo; pafupi chabe monga izo ziriri tsopano. Davide anathawira mu malo aang’ono awa, mu kakhumbi kakang’ono aka, kulikonse kumene iye akanakhoza kupita, malo amphamvu aang’ono omwe iye akanakhoza kugwirako. Ndiye iye anakwera pamwamba pa phiri, pa chirimwe chotentha icho, chapakati, pamene kutentha kunali kwakukulu, ku mmero kwake kukuwawuka, ndipo kukhumudwa ndi mantha mu mtima mwake, ndipo akudabwa, “O Mulungu, zingakhoze kukhala chotani izo? Inu munatsanulira mafuta awo pa ine, osati chifukwa chakuti ine ndinadzisankha ndekha, koma Inu munandisankha ine. Chifukwa chiyani Inu munandiyitana ine kuchoka kolishya nkhoa kutsidya uko, ndi kundiuza ine kuti Inu mudzandipatsa ine izi kuti nditumikire anthu Anu, ndipo apa Inu mwanditengera ine pakati pa moto paliponse?” Izo zinali kupita kupyola mu mtima wake.

<sup>98</sup> Iye anakhala pa phiri ndipo anayang’ana pansi, ndipo apo Afilisti anali atalowa mkati ndipo anazungulira mu Betelehemu momwemo, nyumba yake yaying’ono. Ndiye, mzinda wake wawung’ono unali pansi pa boma la ulamuliro wa mdani. Osati kokha icho, koma nyumba ya atate ake omwe, nyumba ya a Jese, inali pansi pa usinga wa Afilisti. Panali fuko lake lomwe, mpingo wake womwe, ukumutsutsa iye. Apa panali mdani yemwe iye anali kumumenya, apa pali anthu a mpingo womwe iye anali kuwamenya; osati chifukwa chakuti iye amafuna, koma chifukwa chakuti iye anakakamizidwa kuti achite icho.

<sup>99</sup> Ndipo nthawi zambiri ife timakakamizidwa kuchita zinthu ndi kunena zinthu zomwe ife sitikufuna kunena, mtsogoleri weniweni wauzimu, koma iye amakakamizidwa kuti achite izo. Iye ayenera kutenga mbali yake ndi kusonyeza maanga ake. “Ine ndidzatenga njira ndi onyozedwa apang’ono a Ambuye,” anatero wolembe nyimbo.

<sup>100</sup> Koteri apo iye anali, pa tsiku lotentha, mosakaika, akuyenda mmbuyo ndi kutsogolo, ndipo akuyang’ana pansi kupyola chigwa chachitali icho, cha pafupi mailosi makumi awiri ndi asanu pansi apo, ndi kumbuyo. Apo panali nyumba ya atate ake omwe mu—mu singa kwa Afilisti. Apo panali Saulo akuwoloka kumene kutsidyako, n . . . ndipo apa panadza mmodzi uyu, atakhala pakati pomwe, onani, kudzatenga mbali. Powona nthawi yayikulu imene Israeli anali yense atasweka, mpingo unasweka mu zipembedzo zosiyana, mwa kulankhula. Apa panali Davide atayima kumbuyo uku, osadziwa choti nkuchita,

ndipo komabe osadziwa kuti pa iye panali kudzoza. Iwo ankadziwa kuti kudzoza kunali pamenepo. Iwo ankamudziwa Davide anali woti adzakhala mfumu. Aleluya!

<sup>101</sup> Ife tikudziwa Amene ati akhale Mfumu. Ziribe kanthu yemwe ati akhale Purezidenti. Ine ndikudziwa Amene ati akhale Mfumu. Iye adzakhala Mfumu. Ndipo ine ndikudziwa kuti icho chimatengera chinachake kuti chiyime. Koma Mulungu andithandize ine kuti nditseke maso anga kwa zipembedzo ndi china chirichonse, ndi kuyang'ana ku mawonekedwe auzimu awo kutsidya, kuti Iye ali Mfumu yakudza. Ine ndidzamutumikira Iye. Ngati iyo ili imfa, ndiroleni ine ndife; ngati ndi banja langa, ndi okondedwa anga, ngati chiri chipembedzo changa, ndi chirichonse. Ndiroleni ine ndimutumikire Iye. Ine ndidzakhala kwa Iye. Ndiwo ankhondo a Mulungu, monga anali naye Davide, amene anayika manja awo pa lupanga lawo, akuyenda nthawi iliyonse. Ndiwo njira imene ankhondo a Mulungu amayendamo, okonzeka!

<sup>102</sup> Mdani akuti, “Iwe uyenera kumwa pang’ono, kuti uzikhala woyanjanika.”

<sup>103</sup> “Ine sindidzakhudza zinthu zosayera zanu.” Ameni! Apo pali mdani. Apo pali wankhondo!

<sup>104</sup> “O, kodi inu simunyoza chinthu choyera-chodzigudubuza chakale icho chimene inu mumachikhulupirira?”

<sup>105</sup> “Ine ndidzakhulupirira Mulungu. Ine ndidzayima woona!” Ndi zimenezotu. Apo pali ankhondo.

“O, inu mukutanthauzadi? Palibe chinthu chotero chonga machiritso Auzimu!”

“Ndicho chimene inu mukuganiza. Ine ndikudziwa bwino.” Mwaona?

<sup>106</sup> “Palibe chinthu chotero monga Ubatizo wa Mzimu Woyera. Masiku awo adutsa.”

<sup>107</sup> “Ndizo zomwe inu mukuganiza. Ine ndalandira kale Iwo, inu basi mwachedwa kuti mudiuze ine chirichonse za iwo.”

<sup>108</sup> Iwo ankadziwa kuti kudzoza kunali pa mnyamata wakale wamng’ono wooneka-wosakhwima uyo, ndipo iwo ankadziwa kuti iye akhala mfumu.

<sup>109</sup> Koma Davide, mmalingaliro ake omwe, anakhumudwitsidwa. Ine ndikhoza kulingalira, kungomuwona iye miniti, akubwerera kumbuyo uko nakhala pansu, nayang’ana pansu apo, naganiza, “Mzinda wanga womwe wokondedwa, Betelehemu, akuyang’ana pa iwo apo, kumene zinthu zazikulu za Mulungu zinali zitachitikirako, kumene abambo awo abambo abambo anabadwirako; kumene a agogo-agogo-agogo-amayi anga aakazi kutali analankhula mwa iwo, mu nthawi ya kubadwa kwa Yuda, kuchokera kumene fuko lake ine ndikuchokera. Kutaliuko kunali chinachake chazimu.

Iwo analankhula malo awo, ndipo uko Yoswa anamukhazika mwana ameneyo mwa iye kumene. Ndipo kuchokera kumeneko kunabwera zinthu zonse izi apa. Izo ziyenera kutero. Ine ndinali wolishya nkhosa, ndipo Inu munatsanulira mafuta pa mutu wanga. Inu munati ine ndidzakhala mfumu. Ine ndikukukhulupirani Inu. Amenii.”

<sup>110</sup> Ndiye iye akubwerera nayang’ana pansi apo, naganiza, “Chabwino, kutsidya uko mu mzinda wanga wawung’ono, kumene ine ndinabadwirako, gulu laling’ono ilo kumene ine ndinali nawo, masiku abwino akale aja.”

<sup>111</sup> Zikanakhala bwino ngati Amethodisti akanayang’ana mmbuyo ku masiku abwino akale awo, pamene iwo anali apang’ono ndi otalikana pakati mnyumba zazing’ono za sukulu kunja kuno mu America, akugwa pansi pa Mphamvu ya Mulungu, akuponyera madzi mu nkhope zawo. Zikanakhala zabwino kwa inu Abaptisti kuti muyang’ane mmbuyo kumene inu munachokera, inunso, ndi onse a iwo. Inu Apentekoste, yang’anani mmbuyo kumene inu munachokerako. Uko nkulondola.

<sup>112</sup> Mu kutentha kwa nkondo apa, Davide anayamba kuganiza, “O, ine ndikhoza kukumbukira mausiku awo amene ine ndinagona kutsidya ku mbali ya phiri iyo. Ine ndikukumbukira pamene ine ndinaziwona nyenyezi izo, momwe izo zinkasunthira kutali uko, ndi momwe Mulungu analankhulira kwa mtima wa unyamata wanga waung’ono. Ine ndikhoza kukumbukira pamene ine ndinalowa chotero mu Mzimu, tsiku lina, ndikuyang’ana pa mitambo ndi msipu wamthunzi wobiriwira, mpaka ine ndinakuwa pansi pa Mzimu, ndi kuyimba.

*YEHOVA ndiye m’busa wanga; ine sindidzasowa.*

*Inde, ngakhale ine ndingayende mchigwa cha mithunzi ya imfa, ine sindidzawopa choyipa ayi: pakuti inu muli ndi ine; . . .*

<sup>113</sup> O, mai, apa iye anali kumene mu nsagwada za imfa pomwepo, kumbali zonse. “ ‘Inde, ngakhale ine ndingayende kupyola chigwa cha mthunzi wa imfa.’ Masiku abwino akale aja pamene Mzimu unali ndi ine, pamene Mulungu anali ndi ine; ine ndinkayimba matamando Ake, ine ndimasangalala naye Iye.

<sup>114</sup> “Ine ndikukumbukira nthawi yina imene mkango unabwera, mmawa wina, ndi kutenga imodzi mwa nkhosa zanga. Ndipo Mzimu wa Mulungu unadza pa ine, ndipo ine ndinatuluka ndi kuwugwira iwo ndi kuwudula iwo mzidutswa. Ine ndikukumbukira chiwombolo chija. O, ine ndikhoza kukumbukira usiku uja dzuwa lisanalowe kumene, chimbalangondo chinabwera mkati ndi kutenga imodzi, ndipo ine ndinachipha icho. Chiwombolo chachikulu icho!

<sup>115</sup> “Ine ndikukumbukira pamene ine ndinayimba matamando Ake mu masiku a ubwana wanga, pamene ine ndinkalishya

nkhosa zanga. O Mulungu, nditengereninso ine ku malo aja. Nditengereninso ine ku chikondi changa choyamba. Nditengereninso ine ndi kundibwezera ine ndodo yanga ya ubusa. Ndbwezerezi ine gulu langa la nkhusa. Ndisiyeni ine ndekha kumbuyo uko, kukakupembedzani Inu.”

<sup>116</sup> Izo, nthawizina ife timaganiza izo, koma ife tiri mukutentha kwa nkundo. Chinachake chiyenera kuchitidwa. Ife tinakhalapo anyamata nthawi yina; ndife amuna aakulu tsopano. Nkundo ikuchitika. Ine ndikukumbukira pamene utuchi wa macheka unatokota pansu, ndipo anthu anakuwa ndi kufuula, ndipo iwe sukanakhoza kufika pozungulira pamalo paliponse apa, kwa anthu, koma siziri choncho lero. Nkundo ikuchitika. O, sali William Branham, mlaliki wamng'ono wachinyamata, panonso; inu muyenera kutulutsa chinachake, inde, bwana, apo payenera kukhala chinachake chosiyana. Nthawiyo yafika. Nkundo ili mkati. Kutentha kwayaka. Nthawi yoti muwomboledwe, anthu, aliyense anapezeka atalembedwa mu Bukhu. Tsopano nthawi yafika.

<sup>117</sup> Davide ndi zokhumudwa zake zonse, akuyenda mmbuyo ndi mtsogolo, ndipo akuganiza, “O, tsiku lotentha ili lero! Whau, o, ndi lotentha kwambiri! O, Saulo akhoza kubwera kuchokera njira *iyi*, Afilisti kuchokera njira *iyi*; ankhondo atazungulira kulikonse, ndipo apa ife tikukhala mkamwa mwa mphanga! Ndipo, komabe, mafuta odzoza ali pa ine. Kodi izo zingakhoze kukhala chotani, O Mulungu, zingakhoze kukhala chotani izo? O, ine ndikukhumba ine ndikanamwa!” Ndiye malingaliro ake akubwerera, komwe uko pa zipata za Betelehemu, uko kunali chitsime. Uko kunalibe chabe madzi onga madzi awo.

<sup>118</sup> Inu mukudziwa, Palestina ali ndi madzi achabe ena. Iwo ali ndi madzi oyipa, ndipo iwo ali nawo ngakhale malungo a madzi akuda, ndi zinthu, mmenemo. Ndipo ambiri a iwo ali madzi a mchere, amene akhoza kukupha iwe.

<sup>119</sup> Koma Betelehemu ndi mpando wamadzi wa chigawocho, nawonso. Uko kunalibe madzi onga amene Betelehemu anali nawo! Davide anakonda kuganiza, “Pamene ine ndinali nditatenga nkhusa zanga ndi kuuyamba mmawa, ine ndidzadutsa pa chitsime chakale icho ndi kumwa. O, momwe amazizirira ndi momwe amakomera, ndi momwe iwo amathetsera ludzu!”

<sup>120</sup> Tsopano kumero kwake, nkoti kudzozedwa, “O, ngati ine ndikanangokhala nacho chakumwa cha madzi!” Tsopano ankhondo ake. . .Ndipo iye anakuwa, mu kusimidwa kwake, “O, ngati wina akanadzandibweretsera ine akumwa kachiwiri kuchokera ku chitsime chakale chija kutsidya ku Betelehemu!” O, atatha kulota mmasiku ake onse aubwana ndi zigonjetso, ndi kumuwona iye mmalo amene iye akukhalapo apa pakati

pa moto, iye anakuwa, “O, ngati winawake akanakhoza kundibweretsera ine madzi kuchokera ku Betelehemu!”

<sup>121</sup> Tsopano, ankhondo ake sankakhoza kumasulira kuganiza kwake, koma, m’bale, iwo ankamukonda iye ndi zonse zomwe zinali mwa iwo. Chaching’ono cha zokhumba zake chinali ulamuliro kwa iwo. Atatu a ankhondo ake amphamvu anasolola malupanga awo, anachoka pa msasawo, nadula njira yawo, mailosi makumi awiri ndi asanu. Davide, mu kupita kwawo, nzosakayikitsa kuti anadabwa, “Ali kuti iwo? Kodi achita chiyani iwo? Kodi iwo akupita kuti? Kodi iwo amadziwa kuti akuyika moyo wawo pa ngozi?” Iwo ali mu nsagwada kumene za imfa, kupyola mzera wa mailosi makumi awiri ndi asanu, akugona mu chiwembu kulikonse, ndipo malupanga akuthwanima, ndipo zishango zikutchinga; koma munthu wawo, m’bale wawo yemwe iwo ankamukhulupirira kuti adzakhala mfumu, ankafuna akumwa.

<sup>122</sup> O, m’bale, ine ndikudabwa ngati ankhondo lero akulolera kudula njira yawo kupyola zamawonekedwe, zokaikira ndi kusakhulupirira, kuti atsitsimuke mu Kukhalapo kwa Ambuye, zokhumba Zake? “Chaching’ono cha zokhumba Zanu; ngati kuli ku Afrika, India, ngati kuli ku msewu, kulikonse kumene kuli! Chaching’ono cha zokhumba Zanu, Ambuye, ndilo lamulo langa. Imfa siyikutanthauza kanthu kwa ine. Kutchuka, mai chimene ine ndiri, chimene ine nditi ndidzakhale, sichitanthauza kanthu, Ambuye. Ndicho kukwaniritsa zokhumba Zanu.” Ndiwo ankhondo amene akuyima pambali ya Iye. “Ngati iwo anditcha ine ‘woyera-wodzigudubuza,’ ngati dzina langa liyipisidwa, ngati iwo andikankha ine mu msewu, izo ziribe ntchito. Chokhumba Chanu ndicho lamulo langa.” Ndiye msilikari weniweni.

<sup>123</sup> Kodi iwo anachita chiyani? Iwo anamenyera njira yawo kupyola mpaka iwo anafika ku chitsime icho. Iwo anamiza chidebe chamadzi. Ndipo apa iwo anabwerera, akumenya, akudula njira yawo kuchokera kumanja mpaka kumanzere, mpaka akubwera ku kukhalapo kwa Davide. Anati, “Ndi awa, m’buye wanga!” O, mai! Chiyani? Munthu amene ananyozedwa, munthu yemwe ankadedwa ndi mpingo, munthu yemwe ankadedwa ndi mfumu, munthu yemwe ankadedwa ndi Afilisti, munthu yemwe ankadedwa kulikonse, pafupifupi. Koma gulu laling’ono lomwe linkatsata iye, iwo ankadziwa kuti iye anali mfumu yakudza.

<sup>124</sup> Lero, ine ndikudziwa kuti ife timayimba nyimbo zazikulu, ife timamanga mipingo yayikulu, ife tiri nazo nyimbo za fuko zazikulu ndi chirichonse, ife timalemekeza kwa Iye monga choncho, koma Yesu anati, “Mu mitima yanu inu muli kutali ndi ine, pakuti inu mumaphunzitsa Chiphunzitso malangizo a anthu.” Lolani Mzimu Woyera ubwere mkati ndi kuchita chinachake mu mpingo, kusonyeza Kukhalapo kwa



Yesu Khristu, iwo adzakukankhira iwe kunjya pakhomo. “Mwa chabe inu mundipembedza Ine. Iwo amapembedza, koma mwa chabe inu mukuchita izo, kuphunzitsa Chiphunzitso miyambo ya anthu.”

<sup>125</sup> Koma apo pali ankhondo amene amamukhulupirira Iye, pali ankhondo amene amayima nacho Icho, ndi kumvetisa kwauzimu, monga mu Betelehemu wamng'ono kutsidya. Mwaona? Ndithudi, izo zinali.

<sup>126</sup> Davide akutenga chidebe chamadzi ichi, iye anayang'ana pa icho, ndipo Baibulo linanena kuti iye anatsanulira icho pa nthaka, anati, “Ambuye, zikhale kutali kwa ine kuti ine ndingamwe iwo, chifukwa awa anga—ankhondo anu anayika pangozi moyo wawo, kuti apite kutsidya ndi kundibweretsera ine madzi awa. Ndi magazi a munthu. Ine sindingakhoze kuchita icho.” Ndipo madzi okoma awa amene iwo anayikira pangozi miyoyo yawo ndi kudutsa kupyola mzera wa mdani kuti apite kutsidya ndi kukatenga, Davide anawatsanulira iwo pa nthaka monga chopereka cha chifuniro-chaulere kwa Ambuye. Iko sikunali kuyipidwa, iko kunali basi kukwaniritsa Malemba.

<sup>127</sup> Chifukwa, ngakhale Yesu, kuchokera ku Betelehemu, ali Mkate wa Moyo, Iye nayenso ali Madzi a Moyo. Ndithudi, iye ali. Ndipo kodi Iye anachita chiyani? Iye anayimiridwa mwa onse Davide ndi ankhondo; chifukwa Iye anali Mfumu, ndipo Iye anali wankhondo Yemwe anadza ndi kuswa kupyola mu mizera ya mdani. Amen! Kugonjetsa imfa, gehena, ndi manda, kutsanulira Magazi Ake Omwe, kuti Yohane 3:16 akwaniritsidwe!

*Pakuti Mulungu anakonda dziko, kotero kuti iye anapatsa Mwana wake wobadwa yekha, kuti yense wakukhulupirira iye asatayike, koma akhale nawo moyo Wamuyaya.*

<sup>128</sup> Ndiyeno Iye sanapereke madzi amene ankayimira izo, koma ine...Iye anali Madzi, kapena kuwonongeka; anthu owonongeka, kuti akakhale nawo Moyo. Kodi Iye anachita motani icho? Kupyolera mu Magazi Ake Omwe, pa kuwatsanulira Iwo kunjya; osati kuwataya Iwo, ndiyo ngozi. Iye anawatsanulira Iwo kunjya mwaufulu pa Kalvari, atatha Iye kuswa kupyola mu mzera uliwonse wa mdani, ndi kusanulira kunjya Moyo wa Magazi Ake, kuti Iye akakhale dengulu la mkate kwa dziko.

Ndipo Kasupe wodzaza Magazi,  
Wochokera mu mitsempha ya Emmanuele,  
Pamene ochimwa alowa pansa pa kusefukilako,  
Amataya madontho a zolakwa zawo.

<sup>129</sup> Ndicho chifukwa Iye anabadwira mu Betelehemu. Ndicho chifukwa Iye anayenera kubwera, chifukwa icho chinali chimake cha mkate, Mkate wa Moyo. Anali chimake cha madzi,

iwo ali chiyani? Madzi a Moyo? Ndipo mwa Yesu munali zonse Mkate wa Moyo ndi Madzi a Moyo, chotero Iye amayenera kubwera ndi kudzabadwira mu Betelehemu.

Iwe Betelehemu wa Yudea, kodi sindiwe wamng'ono pakati pa akalonga onse aakulu? Ndiwe chabe kamlaliki kakang'ono kawamba, ndiwe chabe kanthu kakang'ono; koma kuchokera mwa iwe mudzabwera Wolamulira amene ali wochokera kale, ndi kunthawizosatha kwa nthawizosatha, kuyenda Kwake kwakhala kwa nthawizonse, ndipo kuchokera ku nthawizosatha mpaka ku nthawizosatha.

<sup>130</sup> Ndicho chifukwa Iye anabadwira mu Betelehemu wa Yudea. Iye anamuyangata Iye. Ndipo, m'bale wanga, malo amene Iye akufuna kuti ayangatiridwe lero ndi mu umunthu wanu womwe, mtima wanu womwe, kuti Iye akawonetsere kuchokera kwa inu, Madzi a Moyo kwa anthu akufa, ndi Mkate wa Moyo kwa anthu akufa ndi njala. Iye ali Mkate ndi Madzi a Moyo, zomwe ziri zinthu ziwiri zofunika kwa moyo wa munthu, ndizo mkate ndi madzi. Ndizo zolonjezedwa, ndithudi.

<sup>131</sup> Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu kamphindi chabe, ndipo, mu kuchita chotero, ine ndikufuna chidwi chanu chosagawanika. Kodi inu mwafikako ku Betelehemu, mmawa uno? Ngati inu simunafikeko ku Betelehemu. . .

<sup>132</sup> Iye ankatchedwa Efrata wa Betelehemu, nayenso, Efrata wa Betelehemu. *Efrata* amatanthauza “muzu,” amabwera kuchokera ku mawu akuti h-e-m-p, *hemp* amatanthauza “muzu.” Ndipo boma lalikulu lakale kumeneko linkatchedwa Efrata, chimene chimatanthauza, “ndicho chiyambi cha moyo.” Ndipo Khristu anati, “Ngati inu mukhala mwa Ine, Ine ndine mpesa ndipo ndinu nthambi.” Iye ali Muzu wa Moyo wonse.

<sup>133</sup> Ngati inu simunafikeko ku Betelehemu Efrata, Betelehemu, bwerani mmawa uno ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu, ndipo Iye adzakukhululukirani inu za machimo anu. Kodi inu mungakweze manja anu kwa Iye, ndi kunena, “Ambuye Mulungu, nchitireni chifundo ine tsopano, ine tsopano pano ndikubwera kwa Yesu, ndi mtima wanga wonse. Ine ndikubwera ku Betelehemu Wanu, Madzi ndi Mkate wa Moyo. Ine tsopano ndikumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanga”? Ambuye akudalitseni inu, anyamata aang'ono kumbuyo uko. Ambuye akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu, aang'ono.

<sup>134</sup> Kodi alipo wina, anene, “Ine tsopano ndikubwera; wopanda kanthu mmikomo mwanga. Ine ndikuyima, waludzu, kumero kwanga nkowuma. Ine ndikudabwa kumene ine ndikhoza kupita ndi kukapeza Moyo weniweni. Ine ndikudabwa. Ine ndalowa mipingo. . .” Mulungu akudalitseni inu, mlongo. “Ine ndalowa mipingo, ine ndachita chirichonse chimene ine ndikuchidziwa kuchita, M'bale Branham, koma ine sindinakhudze konse gwero ilo lopereka Moyo weniweni. Ine tsopano ndikubwera, Ambuye,

kuti ndilandire Iwo.” Iye ali pano chifukwa cha inu. Kodi inu mungangokweza dzanja lanu, ndi kunena, “Ndi ine, Ambuye. Ndine amene ndikuyima, ndi wosowa”? Ambuye akudalitseni inu, pamene ife tikupemphera.

<sup>135</sup> O Ambuye Mulungu, uthenga wawung'ono wosweka uwu wobweretsedwa kuchokera ku Malemba, ngakhale mu zophiphiritsa zake zonse, zomwe Inu munayika izo mmenemo; mwina izo zabisika ku maso a anzeru ndi aluntha, ndipo nkuwululidwa kwa makanda onga omwe ati adzaphunzire. Momwe kuti Betelehemu wamng'ono, wamng'ono wa iyo yonse! Mneneri ananena motani izo? “Kodi sindiwe wamng'ono pakati pa akalonga onse?” Koma izo zinamukondweretsa Mulungu kuti abweretse kuchokera mu malo aang'ono osawonekawo, Wolamulira wa Israeli. Ambuye Mulungu, kuchokera ku gulu laling'ono la amene atsukidwa ndi ofiira M...mzere wa Magazi a Ambuye Yesu, Inu mudzabala, kwa gulu ilo, kwinakwake, Ambuye, pa dziko lonse, Khristu kachiwiri, yemwe ati adzalamulire mafuko onse ndi ndodo ya chitsulo.

<sup>136</sup> Ine ndikupemphera Inu, Atate Mulungu, kuti Inu mudzakhala wachifundo kwa aliyense wa ife amene tiripo tsopano, ndipo mulole kuti ife tibwere ku Betelehemu Wanu. “O bwerani, inu nonse okhulupirika,” ife takhala tikuyimba, “bwerani ku Betelehemu.” Ndipo, Ambuye, aloleni iwo kuti awone kuti sikupita ku mzinda wawung'ono kutsidya, womwe nthawi yina unali chophiphiritsa; koma kupita ku chenicheni, Yesu Khristu, Mkatete wa Mulungu ndi Madzi a Moyo.

<sup>137</sup> Ndipo awa amene anakweza manja awo, alandireni iwo mu Ufumu Wanu, tsopano basi, Ambuye, pakuti ndizo mwa chikhulupiriro chawo pamene iwo—iwo alandira Iye, ndizo mwa chikhulupiriro momwe iwo anakwezera manja awo, ndipo ndizo mwa chikhulupiriro momwe ine ndikukhulupirira kuti Inu mumawalandira iwo. Asungeni iwo, Ambuye, ku Betelehemu, kumene iwo sadzasochera konse kapena kuchokapo ngati Naomi; koma mulole, ngati nthawi zifika polimba, mulole iwo akakhale komweko ku Betelehemu. Kudzakhala bwino, pang'ono ndi pang'ono. Perekani izo, Ambuye.

<sup>138</sup> Tsopano ine ndikupemphera kuti Inu mudzakhala wachifundo kwa iwo amene akudwala ndi osautsika. Alipo awo pano, Ambuye, amene akusowa kukhudza Kwanu kwa machiritso. O Ambuye, Inu munabwezeretsa Betelehemu ku ulemmero wake wonse woyamba. Inu munawubwezeretsa iwo mu nthawi ya kusowa chuma, pamene iwo unali kudwala. Inu munawubwezeretsanso iwo, ndi kumubwezeretsa Naomi pa nyengo ya barele. Ndipo tsopano, Atate, ife tikupemphera kuti Inu mudzamubwezeretsa Naomi aliyense, ndi aliyense yemwe ali muno yemwe akusowa. Ine ndikupemphera, Mulungu. O Ambuye, ndi nyengo ya barele kumene, mtanda wa barele waukulu womwe unawonekera, ukubwera

ukugudubuzika kutsika mphiri, kulowa mu msasa wa mdani. Ine ndikupemphera, Mulungu, kuti Inu mudzabweretsa barele wamkulu uyo mmwamba kulowa mu nyumba ino tsopano, ndipo kuti Iwo ukhale chitetezero kwa—matenda a anthu, palimodzi ndi tchimo, ndipo muchiritse munthu aliyense yemwe ali mu Kukhalapo Kwauzimu.

<sup>139</sup> Ine ndikungomverera, Ambuye, mwina ndi kumverera kwa ndekha komwe basi, koma ine ndikumverera kuti Inu muli pafupi, kufupikira kwa Inu tsopano mkati muno. Ine ndikukhulupirira kuti Inu muli muno. Ndipo ine sindikunena izi chifukwa cha anthu; Inu Amene mumadziwa mtima wa munthu. Ine ndikupemphera, Ambuye, kuti mwanjira yina iwo agwire masomphenya, mmawa uno, ngati ankhondo aja, amene Umphamvuzonse Wanu wawukulu, Mphamvu Yanu yayikulu, Kukhalapo Kwanu kwakukulu, Inu chomwe Inu muli, Mwana wa Mulungu, Mfumu, Mmodzi wodzozedwayo, kuti Inu muli pakati pa ife; iwo adzagwira mawonekedwe a Izo, mu miyoyo yawo, nachiritsidwa ku zosautsa zawo. Ine ndikupemphera pemphero ili, pamene ine ndikuziyika izo kwa iwo, mu Dzina la Yesu Khristu, Mwana Wanu. Amen.

<sup>140</sup> Ine ndikukhulupirira Mulungu, Mawu Ake onse, kukhulupirira kuti gawo lirilonse la Mawu Ake liri lodzozedwa Mwauzimu. Ine ndikukhulupirira kuti Iye sali “Ine ndinali,” koma Iye ali “INE NDINE,” Kukhalapo kwamoyo kwa nthawizonse. Ine ndikukhulupirira izo pomwe pano, pakati pa anthu apa.

<sup>141</sup> Inu amene munakweza dzanja lanu, mukapeze inu mpingo, “mukabatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu, kuyitana pa Mulungu, kutsuka machimo anu,” kukhulupirira kuti kudza Kwake kwa posachedwa ku . . . Iye awonekera mu Kudza Kwache Kwachiwiri.

<sup>142</sup> Ine ndikukhulupiriranso kuti Kukhalapo Kwake kuli pano kuti kuchiritse odwala, kuti kupange abwino iwo amene akusowa. Inu simukusowa kuti muzikhala kwenikweni mukupemphereredwa mmodzi-ndi-mmodzi. Ine ndinatsimikizira izo usiku wina, kwa anthu, kuti ine ndinkangofuna kuwasonyeza iwo chimene chinali chitachitika.

<sup>143</sup> Panali munthu wina wamng’ono, yemwe wakhala, akuyang’ana pa ine tsopano, amene anakhala mu bedi kwa masiku. Kummero kwake kunatupa moyipa kwambiri mpaka iye sankakhoza ngakhale kudywa kapena kanthu, malungo ake anali atakwera kwambiri. Ndipo iye anali atawawuza abambo ake ndi amake, “Tumizani, kamtengeni M’bale Branham kuti abwere adzandipempherere ine.” Ndipo mwanjira yina iwo sanafune kundivutitsa ine, chifukwa ine ndinali wotanganidwa. Ndipo basi Chinachake chinanditsogolera ine kuti ndipite ku nyumba yawo.

144 Titakhala pamenepo, iwo anayesera kubweretsa mbale ya mnyamata wamng'onoyo, anali ndi dzira lofewa kwenikweni ndi chinachake chimzake, ndi nyemba zina zofewa atazitakasa, ndipo iye anali kuyesera kuzimeza izo. Iye amazikomba izo pamenepo, kutenga—chala, nazitakasa izo, dzino lake linali litatupa lonse ndipo mafinya akutuluka mwa iwo. Ndipo—ndipo iye amayesera kutakasa izo monga choncho, ndi chala chake, ndi kuyesera kuzibweretsa izo pa mmero wake monga choncho. Ndipo iye analuma pafupifupi kapena kawiri, ndipo iye sanakhoze basi kuti apitirire, ndipo anazisanza izo.

145 Ine ndinali nditakhala pamenepo, wopanda pemphero; pali chabe chinachake chaching'ono, iwe sungakhoze kumuza aliyense chimene chikuchitika. Ayi. Ine ndinati, “Ambuye, Ambuye, ndi pafupi ku mathero a chaka tsopano. Pakubwera, chinachake chatsopano. Ndiroleni ine. Ambuye, kodi ndi ichi icho, ndi ichi icho?” Ndipo mwamsanga pamene ine ndinayamba kuti ndinene izo, ndi kunena tsopano, mu mtima mwanga tsopano, “ine ndikudziwa kuti Inu muli pano,” mnyamata wamng'ono anafikira ndi kudya kwina, ndi kudya kwina, ndi kudya kwina, ndi kudya kwina, nayeretsa mbale yake yonse, nalowa mu galimoto yake nachokapo kupita.

146 O, Iye ndi Mulungu, onani, Kukhalapo Kwake, Kukhalapo Kwake. Iwo samati . . . Izo zimangomulola Iye kukhalapo.

147 Tsiku lina pamene iwo anajambula chotsiriza ichi, chithunzi chaposachedwapa. Pamene ine ndinamuwona Iye atayima apo, ine ndinayang'ana pa icho ndipo ine ndinaganiza, “Chabwino, ine ndamuwona Mngelo wa Ambuye pa izo, ndipo ine ndikudziwa kuti izo zinali zodabwitsa.” Koma pamene iye anajambula ichi! Ndiye pafupi firii koloko mmawa, Iye anandidzutsa ine nandiuza ine zomwe ziti zikhale, nafotokoza izo zonse kwa ine, ndi momwe chida ndi chirichonse, monga anandiwonetsa ine zinthu pa icho zimene ine ndinali ndisanaziwonepo. Ine ndinalowa mkati ndi kukachitenga icho, ndi kuyang'ana pa icho, ndipo apo icho chinali. Ine ndinali ndisanachiwonepo icho kale. O, chinabweretsa kumverera kotani icho kwa ine, chitonthozo, kudziwa kuti Iye alipo!

148 Iye ali pano, Kukhalapo Kwake chabe. Ndipo Kukhalapo kwa Ambuye kunali apo kuti kuchiritse odwala. Kukhalapo kwa Ambuye kuli pano kuti kuchiritse odwala. Kukhalapo kwa Ambuye kuli pano kuti kubweretse kukhudzidwa kwa ochimwa. Kukhalapo kwa Ambuye kuli pakati pa anthu Ake, ndipo Iye ali Betelehemu wa Mulungu, wodzaza Mkate ndi Madzi. Ine ndiri wokondwa kwambiri (sichoncho inu?) kuti ife tiri nawo malo oti tibwere, kudzadya ndi kudzakhala moyo kwa nthawizonse.

149 Tsopano Ambuye akudalitseni inu. Muli nacho chinachake chimene inu mukufuna kunena, m'bale? [M'bale Neville anena, “Ayi.”—Mkonzi.] Tiyeni ife tiyime ku mapazi athu, mphindi

chabe. Nyimbo yathu yakale yobalalikira. “Tenga Dzina la Yesu palimodzi nawe.”

<sup>150</sup> Ndi angati amawakonda Ambuye, tiyeni tiwone inu mukweze manja anu mmwamba. Tsopano inu mutakweza manja anu, tsopano atsitseni iwo ndipo gwiranani chanza ndi winawake amene wayima pambali panu, nenani, “Mulungu akudalitseni inu, wapaulendo. Mulungu akudalitseni inu.” Uko nkulondola, ndiye konse. Chabwino, uko nkuti mudziwane wina ndi mzake. Chabwino.

<sup>151</sup> Tsopano tiyeni tiyang’ane moloza kumwamba ndi kuyimba nyimbo iyi tsopano.

Tenga Dzina la Yesu nawe,  
Mwana wa chisoni ndi tsoka;  
Lidzakusangalatsa ndi kukutonhoza,  
Litenge kulikonse upita.

Dzina lofunika, (Dzina lofunika) O kukoma  
kwake!

Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha  
Kumwamba;

Dzina lofunika, (Dzina lofunika) O kukoma  
kwake!

Chiyembekezo cha dziko ndi chimwemwe cha  
kumwamba. (Tsopano kumbukirani . . .)



*CHIFUKWA CHIYANI BETELEHEMU WAMNG'ONO? CHA58-1228*  
(Why Little Bethlehem?)

Uthenga uwu wa M'bale William Marrion Branham wolalikiidwa mu Chingelezi pa Lamlungu mmawa, Disembala 28, 1958, ku Branham Tabernacle mu Jeffersonville, Indiana, U.S.A., unatengedwa kuchokera pa matepi ojambulidwa ndi maginito nudindidwa mosachotsera mawu ena mu Chingelezi. Kumasulira uku kwa Chichewa kunadindidwa mchaka cha 1995 ndi Voice of God Recordings.

CHICHEWA

©1995 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE  
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS  
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.  
[www.branham.org](http://www.branham.org)